

CHISINDIKIZO CHACHINAYI



Usiku wabwino. Ife tiweramitse mitu yathu tsopano kwa mphindi chabe, kwa pemphero.

² Atate athu Achisomo ndi Akumwamba, ife tikukuyandikirani Inu kachiwiri usikuuno, tsopano, mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti tikupatseni Inu mathokozo chifukwa cha tsiku lina. Ndipo ife tikupempha tsopano madalitso Anu pa msonkhano usikuuno. Mulole Mzimu Woyera ubwere ndi kudzatipatsa ife kutanthauzira kwa zinthu izi zimene ife tikuzifuna mosamalitsa. O Mulungu, mulole kuti izo zikhale zopambana chotero kuti ife tikhoze tonse kuyanjana pozungulira Mawu mwanjira yoteroyo, kuti, pamene ife tizichoka, ife tidzakhoze kumanena, “Kodi mitima yathu siyinatenthe mkati mwathu pamene Iye amayankhula nafe mkati mwa njira?” Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha chimene Iye wakhala ali kwa ife, ndipo tikudalira kuti Iye akhalabe nafe pamene ife tikupitiriza ulendowu, pakuti tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

³ Wokondwa kwambiri kubwereranso mnyumba ya Ambuye, usikuuno, mu msonkhano kachiwiri! Ndipo ife tiri okondwa. Ndine wokondwa kwambiri kuti. . .

⁴ Ndimangoganiza kuti Chimodzi ichi sichikanabwera, koma Icho potsiriza chinadzatero. Ndipo kotero ndine wothokoza kwambiri, kuti pokhala chotsiriza cha okwera pakavalo anayi amenewo, chimene ine ndikuganiza kuti ndi chimodzi mwa Mauthenga aakulu kwa Mpingo pa nthawi ino.

⁵ Ine sindikudziwa chomwe Chimodzi chinacho chiri. Ine ndikungozitenga izo tsiku ndi tsiku, basi monga momwe Iye akuwululira Izo. Ine ndikuyesetsa kuti—kuti ndizipereke Izo, mwa. . . momwe Iye akuperekera Izo kwa ine.

⁶ Kodi inu mukusangalala nawo—nawo mdalitsowu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi inu munazindikira momwe Izo basi, mogwirizana nayo mibadwo ya mpingo imeneyo, basi momwe Izo zikungogwirizanirana ndendende basi mwangwiro ndi iyo? Ndi momwe izo. . . Kwa ine, izo zikusonyeza kuti ndiwo—ndiwo Mzimu Woyera womwewo umene unapereka mibadwo ya mpingo, Mzimu Woyera womwewo ndiye ukupereka Izi, inu mukuona, chifukwa izo zikugwirizana limodzi; zonsezo kuchita kumodzi kwakukulu kwa Mulungu, kudziwonetsera Yekha mu njira zosiyanasiyana.

⁷ Inu mukuzindikira, pamene Iye anadziwonetsera Iyemwini kwa Daniele, mmasomphenya, apo pankakhoza kukhala choyimira cha chinthu chimodzi, monga a—mbuzi mmalo awa, kapena mwinamwake mtengo; ndipo malo otsatira chinkakhoza

kukhala fano. Ndi—ndi—ndi zinthu zomwe Iye anazichita, kuchipanga icho, chinthu chomwecho nthawi zonse, kungokhala wotsimikiza kuti ife tisazadziphonye zimenezo.

⁸ Tsopano, ndithudi ndinali wokondwa mphindi pang'ono pokha zapitazo, Ine ndimayankhula ndi dona wamng'ono wakhala apayu, pafupifupi usinkhu wa zaka eyite-faivi. Ndipo iye...

⁹ Osati kale, basi ndisananyamuke kupita cha kumadzulo, bwanji, uko kunali a—mtsikana wamng'ono ku mtunda uko mu Ohio, amene anali, ine ndikuganiza chomwecho, amene anali akufa ndi siteji yotsiriza ya leukemia. Tsopano, leukemia ndi khansa ya m'magazi. Ndipo, oh, kanthu kakang'onoko kanali, inu mukudziwa, mchikhalidwe choyipa chotero, mwakuti apo panalibe chiyembekezo china kwa iye nkomwe. Iwo anali akumudyetsa iye kudzera mmitsempha, opareshoni. Ndipo kotero iwo anali kwenikweni banja losauka. Ndipo iwo...

¹⁰ Akazi a Kidd, apa, ndi M'bale Kidd, iwo anawauza iwo za Ambuye woyankha pemphero mochuluka kwambiri. Ndipo anasonkhana pamodzi, ine ndikuganiza, ndipo analemba ganyu winawake, ndipo anamubweretsa mtsikana wamng'onoyo kumusiko. Ndipo iye anali mtsikana wamng'ono wokongola kwambiri, pafupifupi, oh, usinkhu wa zaka sikisi, seveni. [Mlongo akuti, "Zaka naini."—Mkonzi]. Zaka naini. Ndipo—ndipo iye anali kumbuyo uko mchipinda. Ndipo a...

¹¹ Ndipo pamene ife tinapita pamaso pa Ambuye, Mzimu Woyera unapereka mawu kwa iye. Ndipo iwo amayenera azimunyamula iye, ndipo amamunyamula iye ndi kukamudyetsa iye, inu mukudziwa, mwanjira imeneyo. Ndipo pamene amanyamuka, iye anali akulirira chitumbuwa, ndipo, chotero, amadyera chakudya chake kudzera pakamwa. Ndipo iwo anamupatsa iye chitumbuwacho, ndipo anangopitirira kumamudyetsa iye mwachibadwa.

¹² Mu kanthawi kakafupi, masiku pang'ono, iwo anamutengeranso iye kwa adokotala. Ndipo iwo... Adokotala mophweka basi sanakhoze kumvetsa. Iye anati, "Ngati kuti icho panalibepo, ngakhale ngati kuti sanali mtsikana yemwe uja." Iye anati, "Bwanji, apo—palibenso ngakhale chisonyezo chimodzi cha leukemia pamenepo, palibepo, palibepo nkomwe." Chotero, ndipo, iye anali akufa. Iwo anali atamulephera kale iye; ankangomudyetsa iye kudzera mmitsempha yake. Iye anali atasanduka wachikas. Inu mukudziwa momwe iwo amakhalira. Ndipo kotero iwo... Ndipo tsopano iye ali ku sukulu, akusewera ndi ana ena, wokondwa basi monga mmene angakhalire.

¹³ Zikundikumbutsa ine za vuto lina la zimenezo. Tsiku lina, ine ndinali nditangobwera kumene kwathu, apo panali... Ngati ine sindikulakwitsa, iwo anali mwinamwake a Episcopal

kapena anthu Achipresbateria, amene anali atamubweretsa mtsikana wamng'ono kuchokera ku Kansas. Ndipo madokotala anali atamulephera iye, ali ndi leukemia. Ndipo iwo anamupatsa iye, ine ndikukhulupirira, masiku anayi okhala moyo; iye anali atafika poyipa kwambiri. Kotero iwo anati iwo angogwiritsa ntchito masiku anayi amenewo pobwera kuno, kudutsa mmakhwawa a chisanu ndi zinthu, podutsa mdzikolo, kuti iye adzapemphereredwe. Ndipo agogo aamuna, munthu wa mawonekedwe abwino kwambiri, wachikulire, anali wa tsitsi la imvi.

¹⁴ Ndipo iwo anali atakhala naye, kale, masiku awiri, kumusi kuno mu motelo yaing'ono. Ine—ine ndikuganiza kuti iyo kulibeko uko tsopano, mbali iyi ya Silver Creek. Ndipo kotero ndinapita kumusi uko usiku umenewo kukamupempherera iye. Iwo unali molawirira kwambiri mmawa. Ine ndinabwera usiku umenewo, kuchokera kunja kwa mzinda, ndipo ndinapita kumeneko. Ndipo bambo wachikulireyo...agogo aamuna anali akuyenda pamenepo. Ndipo, amayiwo, akuyesetsa kuti azimusamalira mwanayo.

¹⁵ Ndipo pamene ine ndinagwada kuti ndipemphere, Mzimu Woyera unawululira kwa ine chinsinsi chomwe chinali pakati pa—pa amayi ndi abambowo, za chinachake chimene iwo anachita. Ine ndinawayitanira iwo kumbali ndipo ndinawafunsa iwo za chimenecho. Iwo anayamba kulira, anati, “Izo nzoona.”

¹⁶ Kenako ndinayang'ana mmbuyo, ndipo ndinamuwona mtsikana wamng'onoyo akulumpha chingwe, akupita, akusewera. Ndipo tsopano mwana wamng'onoyo...Mu pafupifupi nthawi ya masabata atatu, iwo ananditumizira ine chithunzi cha mtsikana wamng'onoyo, atabwerera ku sukulu, akulumpha chingwe, ndipo analibe leukemia, nkomwe.

¹⁷ Tsopano, tsopano, maumboni amenewo ndi mwamtheradi choonadi chodalirika, mwaona. Kotero, Mulungu wathu ndi weniweni kwambiri, mukuona. Iye timangomutumikira Iye ndi—ndi kumukhulupirira Iye. Ndipo—ndipo ine—ine ndikudziwa kuti Iye ndi weniweni.

¹⁸ Tsopano, ine ndikuyesetsa mwakukhoza kwanga kopambana tsopano, ndipo pamene chinachake, mkati, pakati pathu, chikupanga njira Yake kuti chidutse. Ndipo tsopano ife tiyesetsa, usikuuno, mwa chisomo cha Mulungu, kuti titenge Chisindikizo Chachinayi ichi, ndi kuwona chimene Mzimu Woyera uti uyankhule kwa ife, mu Ichu.

¹⁹ Tsopano ndiwerenga chi—Chivumbulutso, mutu wa 6, ndi kuyambira pa ndime ya 7; ya 7 ndi ya 8. Pakumakhala nthawizonse ndime ziwiri; yoyambayo ndi kulengeza, ndipo ndime yachiwiriyo ndi chimene iye anawona.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachinayi, ine ndinamva liwu la chachinayi—chamoyo chachinayi chikuti, Bwera ndipo udzawone.

Ndipo ndinapenya, ndipo taonani kavalo wotumbululuka: ndipo dzina la amene anakhala pa iye (amene anakhala) linali Imfa, ndipo Gehena inamutsatira...iye. Ndipo mphamvu inaperekedwa kwa iwo pa ngodya zinayi za dziko lapansi, kuti azikapha ndi lupanga, ndi njala, ndi imfa, ndipo ndi... zirombo za padziko lapansi.

²⁰ Tsopano, Ambuye atithandize ife tsopano kuti tichimvetsetse Ichi. Ndi chinsinsi.

²¹ Tsopano, kungobwereza pang'ono chabe, kuti tiyike maziko, monga ife tinachitira ndi mibadwo ya mpingo, okwera awa ndi kumatula uku kwa Zisindikizo izi. Tsopano, kotero ife tingozitenga izo mmalingaliro athu, kuyankhula pang'ono mpaka ife titamverera kuti ndiyo nthawi yoyenera kuti tiyankhule.

²² Tsopano, ife tazindikira tsopano, kuti, kumatula kwa Zisindikizo, ilo ndi Bukhu losindikizidwa la Chiwombolo. Ndiyeno Bukhulo ndi lopiringizidwa ngati mpukutu, basi chimodzimodzi monga momwe ankachitira kale.

²³ [M'bale Branham akuwonetsera kupiringiza ndi kusindikiza kwa mpukutu pogwiritsa ntchito zidutsa za pepala—Mkonzi]. Ilo silinali bukhu la mtundu *uwu*; chifukwa ili langobweramo posachedwapa, mabuku a mtundu *uwu*, ku mapeto, oh, ine ndikuganiza zaka handiredi ndi fite, kapena chinachake, thu handiredi. Ndiyeno iwo ankalingizidwa ilo, kenako nkusiya mapeto osamanga. Monga ine ndinakuwuzirani inu momwe ankachitira izo, ndipo Malemba, poti mukazipeze izo, ndi mu Yereimiya, ndi ena otero. Kenako chotsatira chinkapiringizidwa mozungulira, akatero mapeto ankawasiya osamanga, ndipo izo monga *chomwecho*.

²⁴ Ndipo chirichonse chimakhala Chisindikizo. Ndipo ilo linali Bukhu losindikizidwa-kasanu ndi kawiri, ndipo ilo linali... Palibe mmodzi...Pamene iwo anali...Ilo linali Bukhu la Chiwombolo losindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Ndikhululukireni ine.

²⁵ Ndipo, ndiye, palibe aliyense Kumwamba kapena mdziko lapansi, kapena panso pa dziko lapansi, anali woyenera kulitsegula Ilo kapena ngakhale kuyang'ana pa Ilo. Ndipo Yohane analira, chifukwa iye sanakhoze kupeza munthu aliyense...Chifukwa, ngati Bukhu limenelo likanapanda kutengedwa kuchokera mdzanja la Mwiniwake wapachiyambi...Kumene, Ilo linali litatayidwa ndi Adamu ndi Eva, ndipo linabwerera, iwo atatha kulanditsa maufulu awo a Mawu, malonjezo, cholowa chawo.

26 Iwo, kumbukirani, iwo ankalamulira dziko lapansi. Iye anali—iye anali kamulungu kakang’ono, pakuti iye anali mwana wa Mulungu. Ndipo mwana wa Mulungu ndi ka—ka—kamulungu kakang’ono. Tsopano, zimenezo si zosiyana ndi Lembu. Ine ndikudziwa kuti izo zikumveka mwachirendo.

27 Koma Yesu anati, “Ngati inu mumawatcha iwo, amene Mawu a Mulungu ankadza kwa iwo...” Ndipo kodi Mawu a Mulungu amafikira kuti? [Osonkhana akuti, “Aneneri.”—Mkonzi]. Aneneri. “Ngati inu mumawatcha iwo, amene Mawu a Mulungu amafikirako, ‘milungu,’ inu munganditsutse Ine bwanji pamene ine ndikuti Ine ndine Mwana wa Mulungu?” Mukuona?

Ndipo, tsopano, iwo anali milungu.

28 Ndipo anthunu, ngati iwe ukhala utabadwira mu banja la dzina la banja lako, iwe ndiwe mwana, ndipo gawo la abambo ako.

29 Ndiyen—ndiye pamene tchimo linadzalowa mkati, ife tinapeza kuti munthu anawoloka phompho. Ndipo—ndipo magazi a ng’ombe ndi mbuzi, ankaphimba, koma sankachotsa. Kufikira, Bulitchi yeniyeni itadzabwera, imene ikanakhoza kuchotsa banga la tchimo ndi kuliswa ilo kwathunthu mu zidutswa, ndi kulitumiza ilo mmbuyo kwa wopotoza wake wapachiyambi, amene anali Satana.

30 Pamene ilo linabwerera kwa Satana, iye akuyembekezera nthawi yake ya kudzawonongedwa Kwamuyaya. Tsopano, izo zikuwonetsera zimene ife timakhulupirira. Ife timakhulupirira kuti iye mwamtheradi adzathetsedwa kwathunthu ndi kudzawonongedwa.

31 Ine ndimakhulupirira kuti tchimo lidzaswedwa. Ndipo pamene ilo livomerezedwa, pa maziko a Magazi a Yesu Khristu, zimakhala monga ngati kugwetsera dontho la inki yakuda mu mulu wa bulitchi ya Clorox. Iyo imangoliswa ilo mpaka kusanduka mankhwala, ndi kulitumiza ilo kutali mmbuyo kumene ilo linachokerako. Mukuona? Ndipo ndi momwe Magazi a Yesu Khristu amachitira.

32 Kenako, izo zimamuyika munthu kutsidya kwa phompholo kachiwiri, kukakhala monga mwana wa Mulungu. Mukuona? Ndiyen iye—zikatero iye amadzakhala a—a...Bwanji, ngakhale iye...Mphamvu yolenga ya Mulungu imakhala mwa iye. Ndipo, makamaka, pamene Mulungu angakhoze kulamulira icho kuti chichitike, icho chidzachitika. Ndipo ife tikubwerera. Kutu pamene a—a...

33 Mose, pansi pa magazi a ng’ombe; ndipo pamene iye anakomana ndi Kuwala kuja, Lawi la Moto mu chitsamba choyaka chija. Ndipo iye anayima, pansi pamenepo, pa kutuma kumene Mulungu anali atamupatsa iye. Ndipo iye anali mneneri. Ndipo pamene Mawu a Ambuye abwera kwa iye, iye

ankayankhula, ndipo ngakhale zinthu zinkalengedwa ndi Mawu. Mukuona?

³⁴ Tsopano, ngati zimachitika zimenezo pansi pa amenewo, magazi a ng'ombe, nanga kulibwanji Magazi a Yesu? Osati kuphimba; koma kulichotsa ilo, lonse palimodzi. Ndipo iwe nkumayima mu Kukhalapo kwa Mulungu, ngati mwana wowomboledwa. Tsopano, mukuona, Mpingo uli kutali kudutsa muyeso wake wa kakhalidwe. Ndipo ine ndikuganiza, nthawi zochuluka kwambiri, ife timakhala tikufufuza m'malo mongotuluka kwenikweni ndi kukakumana nalo vutolo.

Ndiri ndi chinachake chimene ndikufuna kuchinena, ndipo ine—ine ndidzatero pa nthawi yake.

³⁵ Ndipo tsopano zindikirani kuti pali chinachake cholakwika penapake mmipingo. Ndipo ine ndikuganiza kuti ndiwo machitidwe a chipembedzo amene apotoza malingaliro a anthu, ndi zina zotero, mpaka iwo sakudziwa momwe angachitire zimenezo. Uko nkulondola.

³⁶ Koma ife talonjezedwa kuti Izo zidzawululidwa. Ndipo tsopano pali Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri zomwe Bukhu ili lasindikizidwa nazo. Ndipo Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri zimenezo tsopano . . .

³⁷ Ndipo kenako zikadzati Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri izi zatsirizika, ife tikupeza, mu Chivumbulutso 10, panali Mabingu asanu ndi awiri achinsinsi amene Yohane anatumidwa kuti awalembe, koma kenako analetsedwa kuti awalembe iwo. Ndipo pa nthawi ya Mabingu amenewo, ife tikumupeza Khristu, kapena, “Mngelo akubwera pansi ndi utawaleza, ndipo akudzapondetsa phazi Lake pa mtunda ndi pa nyanja, ndipo akulumbira kuti nthawi inali itatha, pa nthawi imeneyo.”

³⁸ Ndiyeno ife tikupeza—tikupeza pamenepo, kuti mu kuwulula kwa Zisindikizozo, kuti mwa—Mwanawankhosa anali atasiya ntchito Yake ya umkhalapakati monga Wopembedzera, ndipo anali atatulukira tsopano kudzatenga maufulu Ake, zonse zimene Iye anali ataziwombola pa imfa Yake.

³⁹ Ndipo, kenako, panalibe mmodzi akanakhoza kutsegula Bukhulo. Panalibe mmodzi analimvetsa Ilo. Ilo linali Bukhu la Chiwombolo. Ndipo Mulungu Atate, Mzimu, anali nalo Ilo mdzanja Lake, chifukwa Khristu anali pa Mpandowachifumu monga Mkhalapakati, Mkhalapakati yekhayo. Chotero, apo sipakanakhoza kukhala woyera, panalibe Maria, panalibe Yosefe, panalibe kanthu kalikonse, pa guwa limenelo, chifukwa anali Magazi. Ndipo Magazi okhawo a Yesu ndi amene akanakhoza kupanga chitetezero, kotero palibe china chirichonse chikanamakhoza kuyima monga Mkhalapakati. Uko nkulondola. Apo panalibe kanthu kena kalikonse.

⁴⁰ Kotero lingaliro lonse ili la kupembedzera ndi Yuda pa zandale, ndi kupembedzera ndi Cecilia Woyera pofuna

chinachakenso, ndi zamkhutu. Izo sindizo. . . Ine—ine sindikuti anthu amenewo si owona mtima. Ine sindikuti inu simuli owona mtima pochita zimenezo, ngati inu mumachita. Koma, inu mukulakwitsa, ndinu—ndinu owona mtima molakwika. Ndi chirichonse. . .

⁴¹ Iwo amati, “Chabwino, uyu—Mngelo uyu, uyu—uyu anawonekera kwa Bonifer Woyera ndipo ananena *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*. Ndipo iwo ayenera kunena *ichi*.” Ine sindikukayikira zimenezo pang’ono, mmalingaliro anga, koma kuti wina anawona masomphenyawo. Ine—ine sindikukayika koma kuti Joseph Smith anawona masomphenyawo, koma iwo sanali molingana ndi Mawu ena onsewo. Koteri choncho, kwa ine, ndi zolakwika. Mukuona? Izo ziyenera kubwera limodzi ndi Mawu ena onsewo.

⁴² Umo ndi momwe mibadwo ya mpingo, ndi Zisindikizo, ndi zina zonse za Izo ziliri. Ndipo pamene aliyense aganiza kuti ali nawo Mabingu Asanu Ndi Awiri amenewo, ngati izo sizikugwirizana nawo Mawu ena onse, pali chinachake cholakwika. Mukuona? Izo ziyenera kubwera, PAKUTI ATERO AMBUYE, pakuti *Ili* ndi Bukhulo. *Ili* ndi Vumbulutso la Yesu Khristu, mu uthunthu Wake.

Tsopano, ine—ine ndikukhulupirira ndiye kuti Mwanawankhosa anatulukira.

⁴³ Iwo sanadziwe. Yohane anali akulira. Iye sanakhoze kumupeza aliyense, Kumwamba, pa dziko lapansi, chifukwa onsewo anali kumbali ina ya phompholo, mwaona, tchimo. Apo panalibe munthu. . . Ndipo Mngelo, ndithudi, Iye akanakhoza kukhala woyenera, koma, kuwonjezera apo, iye ankayenera kukhala Wachibale. Ankayenera kukhala munthu. Ndipo uko kunalibe chinthu choterocho, chifukwa munthu aliyense anali atabadwa mwa kugonana.

⁴⁴ Zikanamutengera Iye Mmodzi wobadwa popanda zimenezo. Koteri Mulungu Mwiniwake anatenga chimenecho, mu kubadwa kwa namwali, ndipo anadzakhala Emanueli. Magazi Ake anali, chabwino, Amodziwo omwe anali oyenera. Ndiye pamene Iye anadzawoloka phompho ili, Iyemwini, ndi kudzalipira mtengo ndi kudzakhala mulatho wa ife tonse, kenako Iye anadzakhala pansu, kuti akhale Mkhalapakati. Ndipo Iye wakhala akukhala pamenepo.

⁴⁵ Ndipo Bukhulo kwenikweni lakhala lotsekedwa, nthawi yonseyo. Liri pamenepo, koma ilo likadali mu zophiphiritisa. Iwo analiwona Ilo. Ngakhale Yohane analiwona Ilo. Kulengezako, pamene woyamba anatulukira, iye anati, “Kavalo woyera anapita pamenepo; iye anali naye wokwera pa iye; anali nawo uta mdzanja lake.” Icho ndi chophiphiritisa. Icho sichinawululidwe. Ayi. Icho ndi chophiphiritisa chabe. Ndipo, monga munthu aliyense wa pa dziko lapansi, ndizo zonse

zimene iye akanakhoza kunena. Uko nkulondola. Iye akhoza kumapunthwa ndi kumadzandima, nzosakaikitsa, kugunda penapake *apa* kapena *apo*, ndipo patapita kanthawi.

⁴⁶ Koma ife tikupeza, pamenepo, kuti mu Bukhu la Chivumbulutso, “Pa Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, zinsinsi (zinsinsi zonse za ilo) ziyenera kukhala zitawululidwa kale podzafika nthawi imeneyo.” Tsopano, ameneyo ndi Chivumbulutso 10:1-7, kuti Izo ziyenera kuwululidwa molingana ndi nthawi imeneyo, pa nthawi imeneyo pamene Iye anachita zimenezo.

⁴⁷ Kenako Mabingu Asanu Ndi Awiri anayankhula maliwu awo achirendo, ndipo Yohane ankati alembe. Koma, Yohane ankadziwa chimene Izo zinali, koma iye—iye sanazilembe Zimenezo chifukwa iye analetsedwa kuti alembe Zimenezo. Ndizo mwamtheradi, ndipo palimodzi, chinsinsicho. Izo siziri mu chiphiphiritso nkomwe kapena kanthu. Ife tikungodziwa kuti Iye . . . Iko kunagunda, ndizo zonse.

⁴⁸ Ndipo tsopano mukuphunzira izi tsopano, musati muyiwale, tsopano, Lamlungu, kapena Lamlungu mmawa, ife tachotsapo utumiki wa machiritso chifukwa chodzakhala ndi mayankho ku—ku mafunso a anthu. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu mukhale nalo funso pa Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri izi, ngati ilo likukusautsani inu, chinachake chimene inu simukuchimvetsa. Tiyeni tidzakhale nawo iwo pa Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Ndiye ine ndikhoza kudzadziwa, podzafika Loweruka usiku, ngati ali okwanira ku—kuwayankha iwo, kapena ayi, mukuona. Ndiyeno basi tsopano, mukuti, chabwino, za chinthu chinachakenso, kapena, “Kodi ine ndichite *ichi*?” Kapena—kapena, mwina munali ndi loto. Izo, zonsezo ndi zinthu zoyenera, tsopano, kumbukirani. Izo ndi zinthu zoyenera. Koma tiyeni tingokhala pomwepa ndi Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Ndi pamene ife tiripo. Tiyeni . . . Ndicho chimene—msonkhanowu wakonzedwera, Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Tiyeni tikhale pomwepo ndi Zimenezo.

⁴⁹ Ine ndiyenera kumapita kwathu, ndiyenera kukakhala nayo misonkhano ingapo uko kumadzulo. Ine ndidzabwereranso kenako, mu kuposera mwezi pang’ono kapena iwiri, kapena chinachake chonga icho, ndipo mwinamwake Ambuye adzalola kuti ife tidzakhoze kukhala nacho chinachakenso pa zimenezo, mwinamwake msonkhano wa machiritso kapena chinachake ndiye, kapena chirichonse chimene ife tiri . . . chirichonse chimene chiri.

⁵⁰ Kenako ife tiri nawo Malipenga Asanu Ndi Awiri apa, oti atulukirebe, inu mukuona. Ndipo iwo onse akubwera mmenemo, nawonso. Ndi Mbale Zisanu Ndi Ziwiri, mwaona, zoti zitsanuliridwe. Koteri, ndipo izo zonse zidzalumikizitsidwa momwe umu, koma izo zonse zikadali zachinsinsi panobe.

⁵¹ Tsopano, usiku wathawu...Ife tinapeza kuti Chisindikizo Choyamba chinapita pamenepo, ndipo wokwerayo...Ndipo Ambuye...Kotero ndithandizeni ine, sindimazidziwa izo mmbuyomo. Palibe chirichonse cha zinthu izi chimene ine ndimachidziwa konse mmbuyomo. Uko nkulondola. Ndipo ine basi sindikuzidziwa.

⁵² Ndimangopita kumtunda uko, ndi kutenga Baibulo ndi kukakhala pansipo, ndi kukhala pamenepo kufikira pamene Icho chifika potseguka monga chomwecho. Ine ndimangotola cholemba changa ndi kuyamba kulemba. Ndipo ndimangokhala pamenepo, mwinamwake kwa maora, kufikira Icho chitafika—Icho chitatsirizika.

⁵³ Kenako ine ndimabwerera, ndipo ine ndimakafufuza, pamene ine ndikuwona pamene Iye ananena Ichi. Ine ndimaganiza, “Chabwino, zikuwoneka ngati ndinachiwonapo icho penapake.” Ine ndimakatenga bukhu langa lamatanthauzo a mawu, ndimapita kukayang’ana pamenepo. “Kodi pali chinachake chonga Icho? Ndipo apa Icho chiri pomwe *apa*. Ndiye kenako apa Icho chiri cha *apa* kachiwiri. Ndipo apa Icho chabwerera *apa*, ndi mmusi *apa*, ndi cha *apa*.” Ndiye ine ndimangozimangirizira Izo mkati. Ine ndimadziwa kuti ameneyo ndi Mulungu, malingana ngati Izo zikufanana Lemba ndi Lemba. Ndi momwe Izo ziyenera kuchitira. Basi monga ngati kumanga nyumba, miyalayo imayenera kulumikizana, mwala ndi mwala.

⁵⁴ Tsopano, usiku wathawu ife tinali nako kutsegula kwa—Chisindikizo Chachitatu. Choyamba chinali kavalo woyera, ndipo chotsatira chinali kavalo wofiira, ndipo kenako kavalo wakuda. Ndipo tinapeza kuti okwerawo anali wokwera yemweyo, nthawi zonse; ndipo ameneyo anali wotsutsakhristu, kuyamba ndi kuyamba. Iye analibe—analibe korona, koma iye anadzalandira mmodzi mtsogolo mwake. Ndiyeno ife tinapeza kuti kenako iye anapatsidwa lupanga, kuti achotse mtendere pa dziko lapansi, ndipo ife tinapeza kuti iye anachita zimenezo. Ndiye kenako iye analowa umo ndi mbalume za kupereka, mpingo ndi ndalama, poyeza kuti ugule *ichi* ndi ndalama, ndi ndalama ziwiri kuti ugule *icho*. Koma iye analetsedwa kukhudza Mafuta ndi vinyo, zomwe zinali zochepa zomwe zinatsalira.

⁵⁵ Ndiyeno ife tinapereka, tinalekezera usiku wathawu, powonetsera zomwe Mafuta ndi vinyo zinali, ndi mphamvu yomwe Izo zinali nayo. Ndipo ife...Izo mwinamwake zinamveka mwamwano pang’ono, koma ine...izo ziri basi ndendende Choonadi. Mukuona? Tsopano, ife tinalekezera pa...Tiyeni, mphindi pang’ono chabe, tibwerezenso izo tsopano. Ndiyeno ife tinalekezera, pa mphamvu ya vinyo, chimene Mafuta ankayimira, Mzimu. Tsopano, ine ndikuganiza kuti inu nonse munalemba zonsezo. Inu mukazipepa izo pa tepi, ngati inu simunatero. Ndi pamene mungawapeze Malemba,

kuti, Mafuta nthawizonse amaimira Mzimu Woyera. Monga anamwali opusa opanda Mafuta, anamwali ochenjera anali nawo Mafuta, umene uli Mzimu Woyera. Ndiye kenako mpaka mmbuyo, mwa—mwa—mwa aneneri, ndi ena otero. Ndipo tsopano ine. . .

⁵⁶ Zooni, ine sindikuyesetsa kusolola Lembu lililonse mmenemo. Ndipo pali zinthu zomwe iwe sungakhoze ngakhale kuziyankhula; zotenga nthawi yochuluka kwambiri. Koma ine ndimayesetsa kuziyika apa, ndi Malemba ndi zina zotero, zongokwanira kuwapatsa anthu kuchitira kuti ziwapangitse iwo kudziwa ndi kuwona chithunzi cha Izo. Koma ngati iwe ungakhale pansu ndi chimodzi cha Zisindikizo zimenezo, bwanji, mai, iwe ungakhoze kutenga maulaliki a miyezi usiku uliwonse, pa Chisindikizo chimenecho kumene, ndipo komabe osakhoza kuchikhudza Icho nkomwe, mwaona, pa chimodzi cha Izo. Ndipo ndi momwe—kuchuluka kwake kwa Zimenezo. Koma, kungogunda basi mfundo zikuluzikulu za Izo, ndiye inu mukhoza—mukhoza kuwona chomwe Izo zonse ziri.

⁵⁷ Tsopano, monga Mafuta ankaimira Mzimu Woyera, ndiye ife tinapeza kuti mafuta ndi vinyo zimalumikizana mu kupembedza, mwaona, nthawizonse zimakhala zolumikizana mu kupembedza.

⁵⁸ Ndipo vinyo, ine ndinati, chimene chinabwera kwa ine, kuti vinyo amayimira kuti inali mphamvu ya—inali mphamvu ya kukondoweza mwa vumbulutso. Mukuona? Ndipo ndi pamene chinachake chawululidwa. Icho chimapereka kukondoweza kwa wokhulupirira, chifukwa icho chimaperekedwa mwa vumbulutso. Mukuona? Ndi chinachake chimene Mulungu wanena. Ndi chinsinsi; iwo sangakhoze kuchimvetsa Icho, mwaona. Ndipo, pakapita kanthawi, Mulungu amabwera pansu ndi kudzachiwulula Icho, ndipo kenako nkudzachitsimikizira Icho.

⁵⁹ Kumbukirani, ngati Choonadi chawululidwa, Choonadi nachonso chimatsimikiziridwa. Mulungu, mowirikiza, ziribe kanthu kaya munthuyo ndi wophunzira bwanji, momwe iye angakhaliro wanzeru mmalingaliro ake; ngati Mulungu sayikira kumbuyo zomwe iye akunenazo, pali chinachake cholakwika. Mukuona? Kulondola. Chifukwa, iwo ndi Mawu.

⁶⁰ Tsopano, pamene Mose anapita kumeneko pansu pa kudzoza kwa Mulungu, anati, “Mulole ntchentche zibwere.” Ntchentche zinabwera. Anati, “Mulole achule abwere.” Achule anabwera.

⁶¹ Mwaona, nanga bwanji ngati iye akanati, “Mulole ntchetche zibwere,” ndipo izo nkusabwera? Mwaona, ndiye kuti iye—iye sanayankhule Mawu a Ambuye, mwaona; iye anangoyankhula, iye anayankhula mawu ake omwe. Iye akanakhoza kuganiza kuti panayenera kukhala ntchentche. Koma, apo—apo sipanabwere

ntchentche iliyonse, chifukwa Mulungu sanamuuze iye chomwecho.

⁶² Ndipo pamene Mulungu akuwuza iwe chirichonse, ndi kuti, “Iwe upite ukachite *ichi*, ndipo Ine ndikakhala nacho icho, pakuti awa ndi Mawu Anga,” ndipo Iye nkuchiwonetsa icho mu Baibulo, ndiye Mulungu amayima kuseri komwe kwa icho. Ndipo ngati icho sichinalembedwe mu Baibulo, Mulungu amayima kuseri kwa icho, mulimonse, ngati iwo ali Mawu a Mulungu. Mukuona?

⁶³ Ndiyeno ngati icho chiri kunja kwa ilo, icho chimawululidwa kwa aneneri. Ife tikuzindikira kuti zinsinsi zonse za Mulungu zimazindikiritsidwa kwa aneneri, ndipo iwo okha. Mwaona, Amosi 3:7.

⁶⁴ Tsopano, tsopano, mphamvu ya vumbulutso imabweretsa kukondoweza kwa wokhulupirira. Pakuti, mphamvu ya vinyo, vinyo wachirengedwe, imakondoweza. Mukuona? Ndi yakuti—imupangitse munthu, amene yense wafookeratu, kuti akondowedwe. Mukuona? Mukuona? Chabwino, ndiye, tsopano, pali mphamvu ya vumbulutso la Mawu, imapereka kukondoweza kwa chisangalalo kwa wokhulupirira, kukondoweza kwa kukhutitsidwa, kukondoweza kuti Iwo atsimikiziridwa, Iwo atsimikiziridwa.

⁶⁵ Iyo imatchedwa, mu Lemba, monga ife tikufunira kufanizitsa kwa izo, monga “vinyo watsopano.” Ife nthawizonse timafanizitsa kwa izo monga choncho, monga, “Awa aledzera naye vinyo watsopano.” Mukuona? Chabwino. Kapena, “vinyo wauzimu,” Ine ndikuganiza, kutanthauzira kwabwino kwambiri kukanakhala chomwecho. Iko kukanakhala, pa “vinyo wauzimu.” Monga vinyo wachirengedwe amadziwulula yekha mu mphamvu yokondoweza, kotero momwemonso amatero vinyo watsopano, pamene Iye awulula Mawu a Mulungu, amene ali Mzimu. Oh! Tsopano pali a...ndicho...Mwaona, Mawu Iwoeni ndi Mzimu. Inu mukukhulupirira zimenezo?

⁶⁶ Tiyeni tiwerenge izo. Tiyeni tiwerenge izo, Yohane Woyera 6. Tiyeni tingo...Eya, ndiye inu—ndiye inu—simunena kuti, “Chabwino, tsopano, winawake ananena zimenezo.” Tiyeni—tiyeni tiwone Yemwe ananena zimenezo, ndiyeno ife tidziwa ngati icho chiri Choonadi, kapena ayi. Yohane Woyera, mutu wa 6. Ndipo mutu wa 6, ndipo ine ndikukhulupirira ndi ya sikisite...ndime ya 63, chabwino, ine ndikuganiza iyo ili. Inde.

Ndi mzimu umene umafulumizitsa; thupi silipindula kanthu: mawu amene ine ndikuyankhula kwa inu, iwo ali mzimu, ndipo iwo ali moyo.

⁶⁷ Mawu Iwoeni ndi Mzimu. Iwo ali Mzimu mu mawonekedwe a Mawu. Ndiyeno, mukuona, pamene Iwo afulumizitsidwa, kapena kubweretsedwa ku moyo, Mzimu wa Mawu umapita

kukagwira ntchito ndi kukachita. Mukuona? Chifukwa chakuti...

⁶⁸ Tsopano tayang'anani apa. Ganizo liyenera kukhala ganizo ilo lisanakhale mawu. Ndiyeno pamene ganizo liperekedwa, ilo limadzakhala mawu. Tsopano, *ili* ndi ganizo la Mulungu limene Iye waliyika mu Mawu. Ndiyeno pamene ife tililandira Ilo kuchokera kwa Iye, Ilo limadzakhala Mawu.

⁶⁹ Mulungu anawulula kwa Mose choti achite. Mose anachiyankhula icho, ndipo icho chinadzachitika. Mukuona? Ndi zimenezotu, pamene izo kwenikweni zichokera kwa Mulungu.

⁷⁰ Tsopano ife tikupeza, kuti—kuti Iwo—Iwo amakondoweza ndipo Iwo amapereka chimwemwe, chifukwa Iwo ndi Mawu a Mulungu. Ndipo vinyo watsopano, vinyo watsopano amakondoweza...pamene Iye awulula Mawu. Ndiye, amabweretsa chimwemwe chopitirira muyeso, nthawizina. Ife tinadutsa mu zimenezo, kuti iye amabweretsa chimwemwe chotero mpaka iwe umafika posefukira.

⁷¹ Tsopano, ine ndikudziwa kuti pali zambiri zotentheka, ndi anthu akumatengeka. Ine ndikudziwa kuti iwo nthawizina amachita zimenezo pamene nyimbo ikulumphalumphu, ndi chirichonse. Ndipo ine ndikudziwa kuti izo zimachitika. Ndipo ine—ine ndimazikhulupirira zimenezo, nanenso. Koma ine ndawawonapo anthu mu tsikuli pamene, bola ngati nyimboyo ikuyimba, aliyense anali akulumpha ndi kumafuula; koma pamene nyimboyo yayima, izo zimayima. Mukuona? Ine ndikukhulupirira...Chabwino, izo, izo nzabwinobe, momwe ine ndikudziwira, mukuona, bola ngati anthu akukhala miyoyo yabwino. Ndi...

⁷² Koma, tsopano, chimene, iwe ukayamba kubweretsa Mawu! Tsopano, ndicho chinthu chimene kwenikweni chimabweretsa Moyo, ndi Mawu, ndipo iwo amabweretsa chimwemwe cha kukondoweza kwa vinyo watsopano. Mukuona? Inde. Ndipo ndicho chimene chinali pa Pentekoste, pamene Mawu anatsimikiziridwa.

⁷³ Tsopano penyani. Tsopano, Yesu anawauza iwo, Luka 24:49, “Taonani, Ine nditumiza lonjezo la Atate Anga pa inu; koma inu mupite ku Yerusalemu ndipo mukayembekezere kufikira.” Lonjezo la Atate linali chiyani? Yoweli 2:28, bwanji, ife tikupeza kuti, Iye “adzatsanulira Mzimu.” Mu Yesaya 28:19, momwe kukanadzakhala “milomo yachibwibwi, ndi malirime ena,” ndi zinthu zina zonse izi.

⁷⁴ Iwo anapita pamwamba paja. Ndipo monga ife tinadutsira mu zimenezo, mwinamwake wina anati, “Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti ife tayembekezera utali wokwanira. Tiyeni tingochilandira icho mwa chikhulupiro.” Icho chinali

chiphunzitso chabwino cha Baptisti, koma icho sichinagwire ntchito ndi abale amenewo.

⁷⁵ Kotero ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, icho chinkayenera kukhala chenicheni. Ndipo iwo anayembekezera pa utumiki wawo, kuti Mawu atsimekiziridwe. Ndipo pamene iwe ubwera kudzafuna Mzimu Woyera, iwe uchite chomwecho.

⁷⁶ Inde, iwe ukhoza kuwuvomereza iwo mwa chikhulupiriro. Iwe uyenera kumuvomereza Khristu mwa chikhulupiriro. Ndiko kulondola ndendende. Ndipo iwe umawuvomereza Mzimu Woyera mwa chikhulupiriro; koma kenako muwulole Mzimu Woyera kuti ubwere ndi kudzapereka mdulidwe, monga umboni wakuti Iye wavomereza chikhulupiriro chako, mukuona. Ndiye, mwaona, “Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo chinawerengedwa kwa iye kukhala chirungamo.” Koma Mulungu anamupatsa iye chizindikiro cha mdulidwe, ngati chitsimikiziro chakuti Iye anali atalandira chikhulupiriro chake.

⁷⁷ Kotero ndicho chinthu chomwecho chimene ife tiyenera kuchita. Ife tiyenera kuyembekezera pa Mzimu Woyera mpaka Iwo utachita chinachake; osati kwenikweni chifukwa chakuti ife tinayankhula mmalirime, osati chifukwa chakuti ife tinavina, kapena kuti tinatengeka, ife tinafuula. Kufikira ife titasinthidwa; mpakana pamene chinachake kwenikweni chinachitika! Ine sindikusamala kaya iwo ulowamo mwa mawonekedwe anji. Basi bola ngati icho chinachitika, ndicho chinthu chenichenicho. Mukuona?

⁷⁸ Ndipo ine ndimakhulupirira kuti kuyankhula mmalirime ndi zinthu zina zonse izi ndi zabwino bwino, koma kungoti izo pa zokha sizingagwire ntchito. Ndipo inu mukudziwa kuti izo sizingagwire ntchito. Kotero, izo sizimachita izo.

⁷⁹ Ine ndawawonapo afiti aakazi akuyankhula mmalirime, ndawawonapo afiti aamuna akuyankhula mmalirime ndi kumavina mu mzimu. Ndithudi. Kuyika pensulo pansu ndipo iyo nkumalemba mmalirime achirendo. Ndipo wina nkutanthauzira izo, uko nkulondola, ndi kumanena zooni. Uko nkulondola. Atalemba ndendende zomwe zinali zitachitika, ndipo izo nkukhala ndendende basi mwanjira imeneyo. Kuwawona iwo akuponyera fumbi pa mutu pawo, ndi kumadzicheka okha ndi mipeni, ndi kudziphimba paliponse ndi magazi a chinyama chakuthengo kapena chinachake, ndipo—ndipo, ndithudi, mwaona, ndi kuyitanira pa mdierekezi. Kotero, mukuona, izo sizimati. . .

⁸⁰ Kuyankhula mmalirime sikumachita zimenezo. “Ngakhale ndingayankhule ndi malirime a anthu ndi a Angelo, ndipo ndiribe chikondi, izo sizindipindulira kanthu. Mwaona, ngakhale ndingakhoze kuchita zimenezo!” Mukuona? Kotero

zinthu zimenezo sizimatanthauza kuti iwe uli nawo Mzimu Woyera.

⁸¹ Koma pamene Iye, Munthuyo, a—Mzimu wachisavundi wa Khristu ukhala Mpulumutsi wakowako, ndi kudzakusinthwa iwe, ndi kudzaponyera malingaliro ako molunjika kumene pa Kalvare ndi ku Mawu awa, chinachake chachitika. Inde, bwana. Chinachake chachitika. Palibe wina adzasowe kukuwuza iwe za chimenecho. Iwe udzachidziwa icho pamene icho chidzachitika.

⁸² Ndipo vinyo watsopano, pamene iye abweretsa vumbulutso, ndiye kuti Iwo—Iwo awululidwa.

⁸³ Ndipo umo ndi momwe zinakhalira pa Pentekoste. Iwo ankadziwa kuti—kuti pankayenera kukhala Mzimu utatsanuliridwa pa iwo, ndipo iwo anayembekezera mpaka ichi chitachitika. Ndipo pamene kutsimikizira kwa vumbulutso kunadzachitika, ndiye kukondoweza kunali pa iwo. Iwo ndithudi anatero. Iwo anafuka nthunzi, nawonso. Iwo, mpaka kunja mmisewu; kumene, iwo ankawopakoti, ndipo ankatseka zitseko. Ndipo iwo anali kunja mmisewu; kumene, iwo anali akuchita mantha nalo gulu la anthu; akulalikira Uthenga kwa iwo! Uko nkulondola. Mukuona? Chinachake chinali chitachitika, chifukwa Mawu owona a lonjezo anali atatsimikiziridwa.

⁸⁴ Tsopano tiyeni tiyimire apa kwa miniti. Ngati icho chinabweretsa kutsimikizika kotero kwa anthu amenewo, kuti iwo—iwo... Pafupifupi aliyense wa iwo anasindikiza umboni wawo ndi magazi awo. Zinalibe kanthu kuti pabwera chiyani potsatira, bola ngati iwo anali ndi moyo, iwo samachoka konse pa Iwo. Iwo ankakhala pamenepo, chifukwa iwo anali Mawu owona a lonjezo, atatsimikiziridwa. Vumbulutso linkatsimikiziridwa. Ndipo iwo ankafa, akusindikiza umboni wawo ndi magazi awo omwe.

⁸⁵ Tsopano tayang'anani pa lonjezo la masiku otsiriza. Ndipo apa ife tikuliwona ilo likutsimikiziridwa pamaso pathu pomwe, ku—kubwera kwatsopano kwa Mzimu Woyera ndi zintchito zomwe Iye ankayenera kuchita, ndipo ife tikuzipeza izo pakati pathu pomwe. Mukuona? Oh, ife tiyenera... Oh, mai! Ife tingamve bwanji? Chinachake chimachitika, ine ndikukuuza iwe, mzanga! Pamene wokhulupirira weniweni, woona, wodzipereka, wokonzedweratu, pamene Kuwala uko kukhudza pa mbewu imeneyo, chinachake chimaphulikira ku Moyo watsopano. Mkazi wamng'ono uja pa chitsime!

⁸⁶ Pamene, ansembe ophunzira aja anali atanena, “Chabwino, uyo ndi mdierekezi. Iye ndi wam'bwebwe. Iye ndi—akungowauza anthu amenewo mwayi wawo. Ndipo iye ali—iye ndi mdierekezi.”

⁸⁷ Koma, pamene, mkazi wamng'ono uja ali ndi mbewu yokonzedweratu iyo! Tsopano kodi inu mukuganiza kuti izo si zoona? Koma Yesu anati, “Palibe munthu amene angadze,

pokhapokha Atate Anga atamukoka iye; ndipo onse amene Atate anandipatsa Ine adzabwera.” Ndipo Iye. . .

⁸⁸ Ndipo wotsutsakhristuyo, mmasiku otsiriza, adzakhala wokhoza. . . Mzimu wotsutsakhristu umenewo umene ife tikuwuphunzira, mu zachipembedzo, ndi kutsimikizira kuti zachipembedzo ndi zotsutsakhristu. Tsopano, kwinako, munthu aliyense amene angachoke pano monga chomwecho, iye, pali chinachake cholakwika, ndipo nkumakhulupirabe kuti kachitidwe kachipembedzo sikali kotsutsakhristu. Pamene, izo zatsimikiziridwa mwamtheradi, kuchokera ku mbiriyakale, kuchokera ku chirichonse chimene chiripo, mpaka kudutsa mu Baibulo la Mulungu ndi china chirichonse, ndi zotsutsakhristu. Ndipo Roma ndi mutu wa zimenezo. Ndipo ana aakazi a mipingo akutsatira konseko. Ndipo onse a iwo adzaponyedwa mu gehena. Uko nkulondola. Kotero ife tikuchiwona chinthu ichi, chotsutsakhristu, mzimu wa icho.

⁸⁹ Ndipo tsiku limene ife tikukhalamo, ndipo, bwanji, ilo liyenera kubweretsa “chimwemwe chosasimbika ndi chodzaza ndi ulemelero.” Mkazi wakale wamng’ono uja, mwamsanga pamene icho chinamukhudza iye, mai, mbewuyo inatulukira!

⁹⁰ Tsopano, kumbukirani, Baibulo limanena, kuti mu tsiku lotsiriza, kuti wotsutsakhristu uyu “akanadzanyenga dziko lapansi lonse.”

⁹¹ Apo pakanadzangokhala chiwerengero chaching’ono chokha, amene maina awo anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Ndipo pamene kutsimikizira koono uko kwa Choonadi chowululidwa cha Mawu a Mulungu kukhudza mtima umenewo, iye adzakhudza madzi, ndipo mpaka kutsidya uko ndi Mzimu Woyera, basi mwamphamvu momwe iye angathere. Ndipo inu simungamuyimitse iye kuchita zimenezo, chifukwa Moyo watsopano wogwirira ntchito.

⁹² Ine ndinali kuyankhula ndi munthu, osati kale kwambiri, anali akuyesetsa kuti akambirane nane, ndipo amati, “Kodi iwe sukuchita manyazi kunena kuti Mulungu analenga miyamba ndi dziko lapansi mmasiku atatu?” Ine. . . Kapena, “. . . mmasiku sikisi?”

Ine ndinati, “Ndicho chimene Baibulo linanena.”

⁹³ Anati, “Chabwino, tiri nawo umboni ndipo tikhoza kutsimikizira kuti dziko lapansi lakhalapo kwa zaka mamillioni ambiri.”

⁹⁴ Ine ndinati, “Izo zinalibe chochita chirichonse ndi icho. Mu Genesis 1:1, Ilo linati, ‘Pachiyambi Mulungu analenga miyamba ndi dziko lapansi.’ Nthawi! Ndizo zonse, mwaona. ‘Tsopano dziko linali lopanda mawonekedwe, ndi lopanda kanthu.’” Ndipo ine ndinati, “Ine ndimakhulupirira kuti mbewu iliyonse inali ikugona momwemo, kuchokera ku chitukuko

china kapena chinachake. Ndipo mwamsanga pamene madzi ananyamulidwapo, ndipo kuwala nkuyikhudza iyo, mitengo ndi chirichonse zinamera.”

⁹⁵ Ndipo chinthu chomwecho ndi munthu, ndi choyimira. Pamene a—a—chifunga chonse chinali chitachokapo, ndipo Choonadi chowululidwa kwa mbewu yeniyeniyoni chitagona pamenepo, iyo inamerabe, ndipo Kuwala kwa Uthenga kutakhoza kudzaikhudza iyo mwa kutsimikizira kooni kwa Mawu, iyo idzakhala moyo. Iyo ili nawo Moyo mkati mwake. Iyo idzakhulupirira. Kunja kwa zimenezo, iyo siyingakhale moyo; iyo ilibe Moyo mwa iyo.

⁹⁶ Maina amenewo analembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi, adzatulukira basi motsimikizika monga chirichonse. Ndipo ndi chifukwa chake Yesu akukhala Pamenepo ndi kumayembekezera ndi ntchito Yake ya umkhalapakati, kufikira mbewu yotsiriza iyo. Ndipo Iye adzadziwa ndendende pamene iko kudzakhudze.

⁹⁷ Monga Dr. Lee Vaile... Ine ndikuganiza iye akadali mu msonkhanowu penapake. Ine sindinamuwone iye kwa masiku. Ine sindikukhulupirira kuti ndinamuwona iye. [M'bale akuti, “Iye ali pano.”—Mkonzi]. Iye ali pano. Chabwino, tsiku lina iye ananditumizira ine pepala ili, lokhudza zomwe Ireniyasi ananena. Chabwino, ine ndinamusankha Ireniyasi, kuchokera kale, kuti akhale mngelo wa m'badwo umene iye analimo. Koma iye anati, “Pamene chiwalo chotsiriza icho cha Thupilo chidzabwera mmenemo,” mu m'badwo wotsiriza uno, “kuyenera kukhala... chinthucho chidzawululidwa pa nthawi imeneyo.” Ndipo apa icho chiri. Izo ndi zoona ndendende. Mukuona? Iye tiri mu tsikulo. Chabwino.

⁹⁸ Ndiye, Pentekoste anali nacho chimwemwe chopitirira. Iwo anakondowezedwa kwenikweni. Ine ndikuganiza, izo zimatero ndi aliyense.

⁹⁹ Tiyeni tingotenga mphindi chabe. Tiyeni tiganize za Davide. Iye—iye yense anakondowezeka, nayenso. Iye anati, “Chikho changa chikusefukira.” Ine ndikukhulupirira iye anali nacho cho—chochitika chachikulu mmoyo wake. Chiyani, nchiyani chinamupangitsa iye kuchita zimenezo? Pamene iye anali mu Mzimu... Pakuti, iye anali mneneri. Iye tikudziwa kuti iye anali. Baibulo linanena chomwecho. Mneneri Davide, tsopano, pakuti iye anali mneneri, ndipo iye anali mu Mzimu, ndipo iye anawona chiwukitsiro. Ngati inu mungafune kuwerenga izo, ziri mu Salimo 16:8 mpaka 11. Iye anati, “Komanso mnofu wanga unapangidwa kukondwa. Mai! Ine—ine ndidzapuma mu chiyembekezo, chifukwa Inu simudzasiya moyo wanga mu gehena; ngakhale Inu simudzalola Woyera Wanu Uyo kuti adzawone chivundi.” Ndipo ine ndikukuuzani inu, chikho chake

chinafika posefukira, chifukwa iye anawona. Ziribe kanthu chomwe icho chinali; oh, iye anawona chiwukitsiro, ndipo iye anali kwenikweni . . . ndipo chikho chake chinasefukira.

¹⁰⁰ Kachiwiri, Davide anali nacho chikho china chikusefukira, mu Samueli Wachiwiri, (pokhala kuti mwatulutsa mapensulo anu), Samueli Wachiwiri 6:14. Uko kunali kadanga kachirala.

¹⁰¹ Iwo anali atatenga likasa. Mdani anali atalowa mkati ndipo analitenga likasa la Ambuye, ndipo iwo anali atalitengera ilo kumeneko ndi kukaliyika ilo pamaso pa Dagoni, ndipo Dagoni anagwa pa nkhope yake. Ndipo analitengera ilo ku mzinda wina, ndipo miliri inabuka. Icho chinali . . . Icho chinali chinthu chotentha kwambiri chimene iwo anayamba akhala nacho mmanja mwawo, kumusi uko. Ndipo iwo sankakhoza kulichotsa ilo, chifukwa ilo linali litachoka pamalo ake.

¹⁰² Tsopano, pamene anadzaliyika ilo pa ngolo ya ng'ombe, ndi kuyamba kubwerera. Ndipo pamene Davide analiwona likasa likubwera, inu mukudziwa chimene iye anachita? Iye—iye anadzazidwa kwambiri, ndipo chikho chake chinayamba kusefukira; kukondoweza! Pamene iye anawona Mawu akuwululidwa akubwerera mu Israeli kachiwiri, iye anavina mu Mzimu, ponsepo kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, monga chomwecho. Eya. Chikho chake chinayamba kusefukira, mukuona. Chifukwa chiyani? Iye anawawona Mawu akubwerera.

¹⁰³ Ndipo ine ndikuganiza kuti icho chingamupangitse aliyense kukondowezeka pang'ono pamene iwo akuwona, zitatha zaka zonsezi; ndiyeno Mawu owona, mwa lonjezo lomwe iwo akanati adzakhale, akubweretsedwa ndi kutsimikiziridwa. Ndi nthawi yotani! Ndi nthawi yotani!

¹⁰⁴ Tsopano tiyeni tiwerenge. Ine—ine ndikayamba kumangoyankhula, ine sindifika ku izi, ndipo ine ndikhala nanu nonsenu muno mpaka hafu pasiti teni. Ine ndinakutulutsani molawirira usiku wathawu, kotero ine ndiyenera kukusungani inu kwa nthawi yotalika yabwino usikuuno. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Eya. Eya. Ayi, ine ndimangokuserewulani inu. Mukuona? Ndine . . . Ife tikungofuna basi mmene Ambuye ati atitsogolere. Tsopano:

*Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachinayi,
ine ndinamva liwu la chamoyo chachinayi chikuti,
Bwera . . . udzawone.*

¹⁰⁵ Tsopano, “Pamene Mwanawankhosa anatsegula Chisindikizo Chachinayi.” Tiyeni tiyimire pamenepo tsopano. Chisindikizo Chachinayi, tsopano, Ndani anachitsegula Icho? Mwanawankhosa. Kodi analipo wina aliyense woyenera? Palibe mmodzi aliyense akanakhoza kuchita zimenezo. Ayi. Mwanawankhosa anatsegula Chisindikizo Chachinayi.

¹⁰⁶ Ndipo cha—Chamoyo chachinayi, cholengedwa Chamoyo chonga mphungu, chinati kwa Yohane, “Bwera, udzawone chimene chinsinsi chachinayi cha dongosolo la chiwombolo, chakhala chitabisika mu Bukhu ili,” chifukwa Mwanawankhosa anali kutsegula Ichu. Mwakuyankhula kwina, ndicho chimene iye anali kunena. “Pali chinsinsi chachinayi apa. Ine ndakuwonetsa iwe, mu chiphiphiritso. Tsopano, Yohane, ine sindikudziwa ngati iwe wamvetsa Izo, kapena ayi.” Koma, iye analemba chimene anachiwona, koma icho chinali chinsinsi. Kotero, iye analemba chimene iye anachiwona.

¹⁰⁷ Mwanawankhosa anali kumatula Zisindikizozo, ndipo Mulungu sikuti amati aziwulule Izo. Izo zinasiyidwira kwa masiku otsiriza. Mukuona? Tsopano, tinali ndi ziphiphiritso, ndipo tazifufuza izo, ndipo timachita mwabwino kwambiri nthawizina, mwaona. Koma ife tikudziwa kuti Izo zakhala zikusunthirabe mtsogolo. Koma tsopano, mmasiku otsiriza, ife tikhoza kuyang’ana mmbuyo ndi kuwona kumene Izo zakhala ziri. Ndipo izo zikuyenera kuchitidwa, izo, pa mapeto a m’badwo wa mpingo, basi Mkwatulo usanachitike.

¹⁰⁸ Momwe wina angawutengere Mpingo kudutsa mu Chisautso, ine sindikudziwa. Koma Iwo udutsiranji mu Chisautso, pamene Iwo ulibe—ulibe tchimo? Ine ndikutanthauza... Ine sindikutanthauza mpingo; mpingo udzadutsa mu Chisautso. Koma ine ndikuyankhula za Mkwatibwi. Mkwatibwi, ayi, Iye alibe tchimo lomutsutsa Iye, nkomwe. Ilo linachotsedwa kale ndi bulitchi, ndipo palibe ngakhale a—a... Palibe ngakhale fungo la ilo, ndipo palibe kanthu katsalirapo. Iwo ndi angwiro, pamaso pa Mulungu. Ndiye Chisautso chirichonse nchachiyani kuti chiwayeretse iwo? Koma enawo adzatero. Mpingo udzadutsa mu Chisautso, koma osati Mkwatibwi.

¹⁰⁹ Tsopano, tsopano ife tinangozitengera izo mu ziphiphiritso za mtundu uliwonse tsopano. Monga—mpingo, Nowa, mtundu wonyamulidwira pamwamba, anapitirira mpaka mu tchimo. Mwaona, tsopano, iwo anachita kupita pamwamba. Koma, Enoki anapita poyamba, icho chinali choyimira cha oyera amene adzakalowe, ndipo isanafike nthawi ya Chisautso.

Tsopano tikupeza kuti, Mwanawankhosa uyu anatsegula Chisindikizochu.

¹¹⁰ Tsopano, Chamoyo choyamba chimene ife tikuchipeza, ngati mungazindikire, Chamoyo choyamba chimene ife tinachipeza, chinali a... Chamoyo choyamba chinali mkango, Cholengedwa chamoyo; tinazipeza zimenezo mu bukhu la zisi... la mibadwo ya mpingo. Ndipo kenako Chamoyo chachiwiri, ine ndikukhulupirira, chinali—nkhope ya ng’ombe, kapena mwana wa ng’ombe. Ndipo Chamoyo chachitatu chinali nkhope ya munthu. Koma Chamoyo chachinayi chinali nkhope ya mphungu. Tsopano ndi momwe ndendende ife tinazipezera

izo, zikusinthana ndendende basi monga chomwecho. Ndipo ndi momwe ndendende izo zayikidwira ngakhale mu Bukhu apa.

¹¹¹ Ndiyenso monga mphunzitsi wamkulu, pa nthawi ina mu Florida, akuphunzitsa, akunena kuti—kuti...kuti, “Bukhu la Machitidwe linali chabe mwawamba—ntchito yamiyanga kwa—kwa Mpingo. Mpingo unapezeka mu Mauthenga anayiwo.”

¹¹² Ndipo ife tikupeza, motsemphanitsa kwa zimenezo, kuti ndi Mauthenga anayi amenewo amene akulondera Bukhu la Machitidwe. Ndi kuchokera m’Mauthenga anayi amenewo mmene Bukhu la Machitidwe linalembedwa, machitidwe a Mzimu Woyera mwa atumwi. Ndipo ife tikupeza, cha mu Bukhu umo, kuti olondera amenewo anali kukhala pamenepo akuyang’ana; kummawa, kumpoto, kumadzulo, ndi kummwera. Mukukumbukira momwe ife tinazijambulira izo apa? Ndipo momwe mokongola ndi mwangwiro chirichonse chinagundira basi pamalo ake!

¹¹³ Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire. Anati, “Bwera ndipo udzawone.” Yohane...Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire kachiwiri, ichi chisanachitike. Tsopano, ichi apa ndi chotsiriza cha okwerawo, kuti chidzawulule kuchita kwa wotsutsakhristu.

Mawa usiku, tidzagunda miyoyo ya pansi pa guwa.

Usiku wotsatirawo, ziweruzo.

¹¹⁴ Usiku wotsatirawo, kupita, kwa—kwa mapeto a m’badwo, mapeto a nthawi, a zinthu zonse, mwaona, pamene Iye akutengedwera mmwamba. Chotero, mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri momwemo, mukutsanuliridwa Mbale, ndipo zina zonse zikutsanuliridwamo. Chomwe izo ziri, ine sindikudziwa.

¹¹⁵ Zindikirani. Koma tsopano, pa ichi apa, ife tikupeza kuti munthu uyu apa ndi mphungu, munthu uyu amene... kapena Chamoyo cholengedwa ichi chimene chatsanuliridwa apa tsopano. Kapena, mwa kuyankhula kwina, pali mibadwo inayi yosiyanasiyana ya Izo. Kunali m’badwo wa mkango. Ndipo, ife tikupeza kuti, uwu ukukhala m’badwo wachinayi.

¹¹⁶ Ndipo iye anati, “Bwera ndipo udzawone chinsinsi chachinayi cha Bukhu la Chiwombolo, chimene chakhala chitabisika mu Bukhu ili. Bwera, udzawone.” Ndipo Yohane anapita kukawona, ndipo iye anawona kavalo wotumbululuka. Ndipo, kachiwiri, wokwera yemweyo pa kavalo wotumbululuka uyu.

¹¹⁷ Tsopano iye ali ndi dzina lotchedwa Imfa. Tsopano zindikirani. Palibe mmodzi wa okwera enawo, kapena palibe mmodzi wa akavalo enawo, kapena palibe nthawi imene wokwera uyu anakwerapo, iwo analibe; munthu ameneyo analibe dzina. Koma tsopano iye akutchedwa Imfa. Ilo

silikutchulidwa. Mukuona? Iye akuwululidwa tsopano. Chimene iye ali ndi imfa.

¹¹⁸ Chabwino, momwe ife tingachedwere pa zimenezo kwa ulaliki, ndi kuzipangitsa izo kumveka bwino kwenikweni! Koma chirichonse chimene chiri chotsutsa, chimene chiri chotsutsa chenichenicho, chiyenera kukhala imfa. Chifukwa, pali mitu iwiri yokha, ndiyo, Moyo ndi imfa. Ndipo izo zikutsimikizira kuti vumbulutso la Mzimu Woyera la izi, mu tsiku lino, ndiro ndendende Choonadi. Wotsutsa, iye ndi imfa. Chifukwa, Mawu, monga ife titawonere patsogolo apa, ndi Moyo. Mukuona?

¹¹⁹ Ndipo munthu uyu akutchedwa Imfa. Tsopano, sizinatchulidwe mu nthawi zinazo, za wokwera uyu. Koma, pakuti, tsopano ilo likutchulidwa, kuti iye akutchedwa Imfa.

¹²⁰ Koma pansi pa vumbulutso la mkango...Tsopano yang'anani. Tsopano ine ndikufuna ndiwerenge izi mwacheru, kuchitira kuti ndikhale wotsimikiza; ndinalamba pa malo enaake, ukaime apa. Pansi, osati pansi pa vumbulutso la m'badwo wa mkango, kapena la m'badwo woyamba, m'badwo woyambirira, Ili linali lisanawululidwe. M'badwo wotsatira unali m'badwo wa ng'ombe, umene uli m'badwo wa mdima, m'badwo wapakati, izo sizinawululidwe kuti Ichu chinali chiyani. Ngakhaleenso Chamoyo chonga munthu, cha nzeru, kuyimira okonzansowo, Luther ndi Wesley ndi ena otero, Ichu chinali chisanawululidwe. Koma mu m'badwo wa mphungu, m'badwo wotsiriza, m'badwo wa uneneri, mmene muyenera kudzawuka kuyankhula kwauneneri, mwaona, kwa amene zinsinsi nthawi zonse zimafikirako! Tsopano apo ndi pamene ife basi. . .

¹²¹ Ife tikhalitsa pamenepo kwa kanthawi pang'ono, usikuuno, kuchitira kuti inu mumvetsetse bwinobwino. Tsopano, mu nthawi zambiri, inu mukuzindikira, izi...Ine sindikungoyankhula kwa gulu ili pano. Matepi awa amapita konsekonse, mwaona, ndipo ine ndiyenera kuzipanga izo momveka bwino. Chifukwa, winawake adzatenga tepi imodzi yokha, ndiyeno, ngati iwo sadzatenga ena onsewo, iwo onse adzakhala mmalere, mwaona. Mulungu analonjeza Izi, mwaona, kwa tsiku lino, kwa wotsiriza, kutsirizika kwa zinthu zonse zosiyanasiyana izi zimene zapita ndipo zakhala zitasakanizidwa. Ife tiri. . .

¹²² Ife takhala nazo zovala za Eliya. Ife takhala nayo mikanjo ya Eliya. Oh, pakhala pali anthu amene...John Alexander Dowie anaikidwa mmanda kumeneko, atakulungidwa mu a-mkanjo. Iye ankati iye anali Elisha. Ndipo ife takhala nayo mitundu yonse ya zinthu monga zimenezo. Ndi chiyani zimenezo, mulimonse? Izo ndi zongoti zichotse Choonadi chimene chiti chidzaperekedwe. Mukuona? Iwo anali nawo akhristu onyenga isanafike nthawi ya Yesu. Mukuona? Iwo

nthawizonse amachita zimenezo. Ndi Satana, akuthamanga ndi chokopera, kuti akasokoneze malingaliro ndi chikhulupiriro cha anthu, chinthucho chisanachitike kwenikweni. Ndizo zonse.

¹²³ Kodi Gamalieli sananene chinthu chomwecho kwa Ayuda tsiku lijali? Anati, “Kodi sanawuke munthu, amene ankadzinenera kuti anali Ichi? Ndipo iwo anawatengera foro handiredi kupita mu chipululu. Iwo anawonongeka, ndi zina zotero.”

¹²⁴ Anati, “Nthambi iliyonse imene Atate Anga a Kumwamba sanaibzale,” Yesu anati, “idzazulidwa.”

¹²⁵ Gamalieli anati, “Asiyeni iwo okha. Ngati iwo, ngati icho sichikhala cha Mulungu, kodi icho sichidzafika posakhala kanthu? Koma ngati icho chikhala cha Mulungu, inu mudzapezeka mukumenyana ndi Mulungu.” Munthuyo ankagwiritsa ntchito nzeru. Iye anali mphunzitsi.

¹²⁶ Tsopano zindikirani. Tsopano, kuti titsirizitse zinsinsi zonsezi, Mulungu walonjeza kuti pakanadzakhala Elisha weniweni adzawuke, munthu wina wodzozedwa ndi Mzimu umenewo, ndipo adzawulula. Iye analonjeza zimenezo mu Malaki 4. Ndipo ine ndiri nazo zolembe ndi makalata zomwe zikunena kuti izo siziri chomwecho, koma ine ndikufuna ndidzayankhule naye munthu ameneyo. Mukuona? Bwanji, iwe sungazikane zimenezo. Wazafioloje weniweni, wabwino amadziwa kuti ndi Choonadi, kuti iwo akuyembekezera izo.

¹²⁷ Koma kungokhala mwanjira yomweyo monga izo zinabwerera ndi Yohane, wotsogolera wa nthawi yoyamba ya Khristu. Bwanji, iwo sanamuzindikire iye, chifukwa panali zinthu zazikulu chotero zimene zinaloseredwa za iye. Bwanji, iye anali woti “adzawapange malo onse okwera kukhala otsika, ndi malo onse otsika kukwera, malo onse okumbika kusalazidwa.” Ndipo, oh, iye... Aneneriwo: Yesaya, zaka seveni handiredi ndi thwelovu kusanachitike kubadwa kwake; ndipo Malaki, zaka foro handiredi asanabwere iye powonekera; onsewo ankaloosera za iye. Ndipo iwo anali kuyembekezera khonde lina la Kumwamba kuti litsitsidwa, ndipo mneneri uyu nkutulukira apo pomwe ali ndi ndodo yake mdzanja lake, akuchokera kwa Mulungu.

¹²⁸ Ndipo chinachitika ndi chiyani? Munthu amene inu... sakanakhoza ngakhale kuwonetsa khadi la chiyanjano. Iye sakanakhoza kuwonetsa chomuyenereza. Ankakhala kutali mu chipululu; wopanda ngakhale maphunziro wamba a sukulu. Iye timawuzidwa, ndi azambiriyakale, kuti iye anapita ku chipululu pamene iye anali ndi zaka naini zakubadwa, itachitika imfa ya abambo ake ndi amayi ake. Ndipo analeredwa... Ntchito yake inali yofunika kwambiri, kuti ayisokoneze ndi seminare inayake. Iye anali—iye ankayenera kuti adzamulengeze Mesiya.

¹²⁹ Mulungu sakanakhoza kumugwiritsa ntchito munthu wokhuthala kwathunthu ndi fioloje. Iye sangakhoze kuchita zimenezo, chifukwa iye nthawizonse azibwerera mmbuyo momwe. Ndiwo mzere wake umene anaphunzirira. Iye azibwerera mmbuyo kwa zimenezo. Chotero, iye akapita kuti akawone chinachake, iye aziyesera kubwerera mmbuyo kwa zomwe aphunzitsi anali atanena. Zingakhale bwino ngati inu mutakhala kutali kwa zinthu zimenezo, ndi kungokhulupirira Mulungu.

¹³⁰ Ndipo ife tikupeza kuti iwo anamuphonya iye. Ngakhale atumwi atayima pamenepo, anamuphonya iye. Bwanji, iwo anati, “Nchifukwa chiyani Lemba limati, alembi, amanena kuti Eliya . . .”

¹³¹ Iye anati, “Chabwino, iye wabwera kale, ndipo inu simunamudziwe iye.”

¹³² Ndipo apo ndi pamene ine ndimafanizira chiwukitsiro, kapena Mkwatulo. Iwo udzachitika, ndipo iwo adza . . . ine ndikudziwa kuti izo zikumveka mwachirendo. Koma mwinamwake inu mudziwa mochulukirapo pang’ono ukadutsa usikuuno, ngati Ambuye alola, basi momwe ziti zidzakhalire, mwaona. Iwo udzakhala mwachinsinsi kwambiri, palibe amene ati adzadziwe za iwo, nkomwe. Dziko lizidzangoganizira, lizidzangomapitirirabe monga ilo nthawizonse lakhala likuchitira, mwaona, ndipo basi . . . Ndi momwe Iye nthawizonse amachitira zimenezo.

¹³³ Inu mukudziwa, ine ndikukayikira ngati mmodzi—mmodzi . . . Ine ndikuti, gawo limodzi pa magawo nainte pa handiredi la anthu pa dziko lapansi, ankadziwa konse kuti Yesu Khristu anali kuno pamene Iye anali kuno. Kodi inu mukudziwa, pamene Eliya ankanenera, ine ndikukayika ngati panali konse aliyense amene ankadziwa kuti iye anali . . . Iwo ankadziwa kuti kunali chidempete kumtunda uko, winawake wotentheka wakale, koma iwo ankamuda iye. Ndithudi. Iye anali chimene iwo ankachitcha wosamvetsetseka.

¹³⁴ Ndipo ine ndikuganiza, Mkhristu aliyense wobadwa kachiwiri amakhala wonga ngati wosamvetsetseka, kwa—kwa dziko, chifukwa iwe wasinthidwa. Ndiwe wochokera ku dziko lina. Mzimu Wako ndi wochokera kutsidya kwa phompho. Ndipo chinthu ichi apa ndi chinthu chosokonezeka chomwecho, chinthu, ndiwe—sindiwe wosiyana, pali chinachake cholakwika; iwe, iwe ukadali womangidwa kwambiri ndi dziko lapansi. Iwe uyenera kukhala wamalingaliro Akumwamba. Ndipo Kumwamba kumakhalidwa moyo mwa Mawu.

¹³⁵ Tsopano, ife tikuzindikira kuti ichi—chinthu chachikulu ichi chinachitika. Tsopano, ife tikukhulupirira kuti kudwabwera Mzimu woona wa Elisha. Izo zinanenedweratu kuti zidzakhalapo, mwaona. Ndipo ife tiyenera kukumbukira

kuti iwo udzakhala kuno, mu nyengo yake yomwe ndi nthawi. Ife tikhoza kukhala kuti tikuyika maziko a iwo tsopano. Ndipo iwo ayi. . . sudzakhala bungwe ayi.

¹³⁶ Ine—ine sindikugwirizana naye mzanga wabwino, pa zimenezo. Iye amanena kuti ilo lidzakhala gulu la anthu. Ine ndikufuna kuti inu mudiwonetse ine izo mwa Lemba. Mulungu, Mulungu wosasintha, samasintha konse madongosolo Ake. Ngati Iye amatero, ndiye Iye si Mulungu; uko nkulondola, chifukwa Iye ndi wachivundi, ndipo Iye amadziwa basi monga momwe ine ndimachitira, ndipo Iye amalakwitsa.

¹³⁷ Mulungu sanasintheapo konse dongosolo Lake, kuyambira mu nthawi yomwe ya m'munda wa Edeni. Iye anapanga dongosolo la chiwombolo; limenelo linali Magazi. Ndipo ife taye setsa maphunziro. Ife taye setsa utsogoleri wankhanza. Ife taye setsa kuwerenga maganizo. Ife taye setsa zazipembedzo. Ife taye setsa chirichonse, kumukankhira aliyense pamodzi, kapena kumukonda aliyense pamodzi, ndi china chirichonsecho. Palibe malo ena achiyanjano koma pansi pa Magazi, apobe, malo okhawa amene Mulungu amakumana naye munthu.

¹³⁸ Mulungu nthawizonse amachita ndi munthu mmodzi payekha. Anthu awiri amakhala ndi malingaliro awiri. Sipanakhalepo aneneri aakulu awiri pa dziko lapansi, akunenera nthawi yomweyo. Yang'anani mmbuyo ndipo mukawone ngati anakhalapo. Ayi, bwana. Kulekelera kochuluka kwambiri! Iye amayenera kumutenga munthu mmodzi wodzipereka kwathunthu, ndi kumugwiritsa ntchito munthu ameneyo. Iye amamufunafuna munthu ameneyo.

¹³⁹ Koma padzakhala mmodzi, nthawiina, winawake amene ati adzamvetsere kwa Iye, Mawu pa Mawu. Ine sindikusamala chimene wina aliyense ati adzanene, iwo sadzasuntha konse kwa Iwo. Uko nkulondola. Iwo adzayembekezera pa PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo, ndiye, iwo sadzasuntha mpaka nthawiyo. Iye adzatsimikiziridwa mokwanira. Inu mudza. . .

¹⁴⁰ Tsopano, dziko lakunja lidzadana nacho icho, koma Mbewu yosankhidwa, Mbewu yokonzedweratu, monga inalipo mmasiku a Yesu, pamene Kuwala kumeneko kudzawala, Mbewu imeneyo idzabwera ku Moyo monga *choncho*. [M'bale Branham akukhwatichitsa zala zake—Mkonzi]. Iwo adzachimvetsa Icho. Iwo adzachimvetsa Icho. Inu simudzasowa kuyankhula liwu lokhudza Icho.

¹⁴¹ Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Ine ndikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, Iye adzayenera. . .”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

¹⁴² Mnyamata, izo, izo zinali zokwanira. Iye sanasowe kuti ayembekezere usiku wonse, ndi kuyembekezera usiku wotsatira. Iye anakhala nacho Icho pomwepo. Iye anali ali panjira yake. Iye anali akuwauza iwo za Icho.

¹⁴³ Tsopano kumbukirani, tsopano, m'badwo woyamba unali m'badwo wa mkango. Uwo unali Mkango wa fuko la Yuda, Khristu. Chikoka Chake Chomwe cha Moyo, chinatenga m'badwo umenewo. Ndicho *Chamoyo* choyamba, chimene chikutanthawuza “Mphamvu,” imene inkayankha mwa liwu la munthu.

¹⁴⁴ M'badwo wotsatira unali m'badwo wa ng'ombe, kapena m'badwo wa wokwera pakavalo wakuda. Mukuona?

¹⁴⁵ Tsopano, chifukwa chimene m'badwo woyamba uwo unali m'badwo woyera, chinali chakuti...Monga—monga ine nthawizonse ndakhala ndikuwamvera anthu akunena kuti wokwera woyamba uyo, woyerayo, anali mphamvu ya mpingo, yomwe inapita kukagonjetsa. Ndipo ife tinapeza kuti iye anapatsidwa korona, kuti uyo anali ameneyo. Iwo unali mpingo. Iwo unali mpingo, koma iwo unapita kuti? Unapita ku Roma. Ndiko kumene iye anakachita. Iye anakalandirira korona wake.

¹⁴⁶ Tsopano, m'badwo wachiwiri unali—unali wokwera pakavalo wofiira, umene unali m'badwo wa mdima.

¹⁴⁷ Ndipo tsopano—tsopano, a—m'badwo wotsatira, unali a—munthu, wa m'badwo umene unali wokwera pakavalo wakuda. Ndipo iye anali m'badwo wa okonzanso, mwaona, pamene a—Liwu limene linkayankhula. Tsopano, wokwera pakavalo wakuda, ameneyo anali wotsutsakhristu. Koma Mmodziyo amene anali kuyankhula mu m'badwo umenewo anayimiridwa ngati munthu, ndipo ndizo nzeru, kuphunzira, kuthyathyalika. Mukuona? Ndipo iwo sanazimvetsetse zimenezo, mwaona. Iwo sanamutche...Iwo sanamutche iye dzina. Mukuona? Iwo anangoti iye anapita.

¹⁴⁸ Koma tsopano, pamene wabwera m'badwo wa mphungu, ndiwo umene...Mulungu nthawizonse amawafanizitsa aneneri Ake ndi mphungu. Iye amadzitcha Iyemwini mphungu. Mphungu imapita mmwamba kwambiri, palibe china chirichonse chingamukhudze iye. Sikuti iye amangokhala kumwamba uko, koma iye anapangidwira malo umenewo. Pamene iye afika mmwamba umo, iye amakhoza kuwona pamene iye ali. Anthu ena amafika mmwamba umo ndipo samakhoza kuwona pamene iwo ali, kotero sizimapanga ubwino uliwonse kufika mmwamba umo. Koma ngati iwe...

¹⁴⁹ Koma inu mumulole khwangwala ayesere kuwuluka limodzi ndi mphungu, kapena mphamba, chimodzi mwa izo, iye akhoza kunyenyeke. Iye ayenera kukhala ndi mapangidwe olimba kuti akwanitse kudutsa kumene iye akupita.

¹⁵⁰ Ndiro limene liri vuto lero, ena a ife sitimakwanitsa kupirira ndi kufinyidwa. Ife timaphulika mwamsanga kwambiri, mukuona, pamene ife tikulumpha. Ndipo, koma, ife timayenera kukhala ndi mpweya.

¹⁵¹ Pamene iwe ufika mmwamba umo, ndi kukhala nako kupenya kwakuthwa kwa mphungu, kuti uwone zomwe zikubwera, ndi kudziwa choti uchite. Tsopano, m'badwo wa mphungu wawulula Ilo. Tsopano ife tikupeza, kuti m'badwo wa mphungu unalonjezedwa mu Chivumbulutso 10:7 ndi mu Malaki...:1, 4. Kuti zikanadzakhala mmasiku otsiriza, mwaona, uko nkulondola, kuti izo zikanadzakhala ziri kuno. Chabwino. Zindikirani.

¹⁵² Tsopano, munthu uyu, ife tikupeza kuti iye akukwera pa kavalo wotumbululuka. Wotumbululuka! Oh, mai! Atatha, zindikirani atatha...

¹⁵³ “Achiprotestanti sikisite-eyiti milioni,” monga ife tinazitengera kuchokera—kuchokera mu *Glorious Reform* la Schmucker, la—la mbiriyakale ya ofera ya Roma, usiku wathawu. Ife tikupeza kuti, mpaka ku chikhomo cha 1500, ine ndikukhulupirira izo zinali, kapena eyitini-...Ine sindikukumbukira bwinobwino tsopano. Koma anali sikisite-eyiti milioni amene anayikidwa ku imfa, amene anawutsutsa mpingo woyamba wa Chiroma, Roma. Nzosadabwitsa, iye anakhoza kudziziyimbaitsa yekha mu dzina laumunthu la... ndi kutchedwa Imfa. Iye ndithudi anali.

¹⁵⁴ Tsopano, Mulungu yekha akudziwa kuchuluka kwake kwa amene iye anawapangitsa kuti afe mwauzimu, mwa kuphunzitsa kwake kotsutsa-Baibulo, kuphunzitsa kwa Mawu! Uyu ndi iye amene anawayika sikisite-eyiti milioni ku lupanga, ndi kuwapha iwo. Ndipo mwinamwake, kwenikweni, mabillioni anafa mwauzimu, pa kuphunzitsa kwake kwabodza. Nzosadabwitsa kuti iye anakhoza kutenga dzina la Imfa!

¹⁵⁵ Mukumuwona wokwerayo? Pamalo oyamba, monga wotsutsakhristu, iye anali imfa, pa kuyamba pomwe; koma iye anali wosalakwa kumeneko. Kenako iye anadzalandira korona, wa patatu; ndipo pamene iye anatero, kenako iye anayanjanitsa, Satana anayanjanitsa mpingo wake ndi boma, chifukwa iye anali pamwamba pa zonse izo pamenepo. Wotsutsakhristu anali Satana, mwa mawonekedwe a munthu.

¹⁵⁶ Ndiyeno, komanso, Mateyu Woyera, ine ndikukhulupirira ali, mutu wa 4, akutiwuzwa ife zimenezo—zimenezo. Satana anamutengera Yesu, Ambuye wathu, pamwamba, ndipo anakamuwonetsa Iye maufumu a dziko lapansi, onse a iwo, mu kamphindi ka nthawi, ndi ulemelero wa iwo, anawapereka iwo kwa Iye. Ndipo iye anati...Iwo, iwo anali ake.

¹⁵⁷ Kotero, mukuona, ndiye, ngati iye angakhoze kuyanjanitsa boma lake ndi mpingo wake pamodzi, ndiye wokwera pakavalo wofiira akanakhoza kukwera, motsimikiza ndithudi. Mukuona? Moona! Tsopano, ndiye, ife tikupeza chinsinsi chake apa, mu mpingo wake ndi boma.

¹⁵⁸ Gawo lachinayi la utumiki wake, iye akutchedwa chirombo. Poyamba iye akutchedwa wotsutsakhristu, mwaona; kenako iye akudzatchedwa mneneri wabodza; ndipo iye akutchedwa chirombo. Tsopano ife tikumupeza iye apa akutchedwa monga chirombo. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire, izo ziri pambuyo pa kavalo wachinayi.

¹⁵⁹ Ndipo mu kavalo wachinayi uyu, ngati inu mungazindikire, zonse... Woyambayo anali woyera; ndipo kenako wotsatirayo anali wofiira; ndipo wotsatirayo anali wakuda; ndipo wachinayiyo, atatu ena onse awa anayimiridwa mmenemu; chifukwa, kutumbululuka ndi kufiira ndi—ndi kuyera, ndipo kotero, kutasakanikirana. Mukuona? Iye... Izo—izo zonse zinasakanizidwa mwa kavalo mmodzi uyu. Mukuona? Ndipo pamenepo iye akukhala anayi, kapena, makamaka, atatu mwa mmodzi. Ndipo izo zonse zinasakanizidwa mwa chinthu chimodzi chimenecho.

¹⁶⁰ Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire anayi a iwo. Zindikirani kuphonya chandamale kwake, kwa zinayi, kwa masamu auzimu. Mulungu amakhala mu zitatu. Izi ndi zinayi. Iye ali mu chachinayi, apa. Poyamba, wotsutsakhristu, woyera; kachiwiri, mneneri wabodza, wofiira; kachitatu, vicar wa miyamba ndi dziko lapansi ndi—ndi purigatoriyo, wakuda; kachinayi, chirombo, kavalo wotumbululuka, Satana ataponyedwa kuchokera Kumwamba. Kodi inu mukufuna kuwerenga zimenezo? Chivumbulutso 12:13, Satana ataponyedwa kuchokera Kumwamba. Kenako mu Chivumbulutso 13:1, 8, iye ali mu thupi la umunthu wa chirombo.

¹⁶¹ Iye poyamba anali wotsutsakhristu, basi—chiphunzitso chabe chotchedwa Chinikolai; kenako iye anadzakhala, kuchokera kwa icho, anadzakhala mneneri wabodza. Ngati iye ali wotsutsakhristu, wotsutsakhristu ndi *wokana*. Chirichonse chimene chiri chotsutsa Mawu a Mulungu chimakhala chotsutsa Mulungu, chifukwa Mawu ndi Mulungu. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anasandulika thupi, Khristu, ndipo anadzakhala pakati pathu.” Ndipo tsopano iye akuwatsutsa Mawu, kotero iye akukhala wotsutsakhristu. Koma mzimu sungavekedwe korona; ndi chifukwa chake iye sanalandire korona. Uta chabe, wopanda mivi.

¹⁶² Ndipo kenako pamene inadzafika, nthawi yovekedwa korona, ndiye iye anadzakhala mneneri wabodza wa chiphunzitso chake chotsutsakhristu. Mukumvetsa zimenezo? Kenako iye akutenga lupanga, chifukwa akuyanjanitsa mphamvu zake pamodzi, ndiye iye sakuyeneranso kumufunsa aliynense. Iye ndi kazembe wa boma; iye ndi kazembe wa Kumwamba. Akulandira korona wa patatu. Iye akudzipangira iyemwini lingaliro lotchedwa “purigatoriyo.” Kumene, ngati—

ngati ena a iwo anamwalira kumbuyo uko, ndipo ali nazo ndalama zina, akufuna kulipira kuti achokeko, iye akhoza kuwapempherera iwo kuti atuluke kumeneko. Chifukwa, iye ali nayo mphamvu yochitira zimenezo; iye ndi *vicar*. Ndithudi, iye ali. “Iye akutenga malo a Mulungu, pa dziko lapansi.” Ngati izo siziri zomveka bwino monga chirichonse!

¹⁶³ Ife tinazipeza izo, tinazikokera izo pansi, kudutsa mu Baibulo, ndi kuwerenga mawerengero ake ndi china chirichonse. Apa iye ali...?... mmbuyo momwe umu mu nambala foro, osati nambala firii. Nambala foro, mwaona.

¹⁶⁴ Tsopano tiyeni titsegule, Chivumbulutso 12. Tiyeni tingowerenga izi pang’ono pokha, chifukwa ife—ife tikhala nayo nthawi yochitira zimenezo. Ndipo tiyeni tiwerenge Chivumbulutso mu—mutu wa 12 ndi ndime ya 13. “Ndipo mu ora lomwelo kunali chivomezi chachikulu...” Ayi, ine ndapeza—ine ndapeza malo olakwika. Ya 13:

Ndipo pamene chinjokacho chinawona kuti chinaponyedwa kunja ku dziko lapansi, icho chinazunza mkazi amene anabala mwana wamwamuna.

¹⁶⁵ Tsopano, mukuona, iye anaponyedwa kunja, pa dziko lapansi, ndipo anadzakhala mu thupi, monga mzimu wotsutsakhristu unadzakhala mu thupi la munthu. Munthu ameneyo akusinthira kuchoka ku chinthu chimodzi nkudzakhala china, kuchoka ku mzimu wotsutsakhristu nkudzakhala mneneri wabodza, ndipo kenako chirombo chikudwabwera mwa iye.

¹⁶⁶ Chimodzimodzi basi monga momwe Mpingo ukukulira; mpingo wake unakula kuchokera—kuchokera pokhala wotsutsakhristu nkudzakhala mneneri wabodza, ndipo, mu m’badwo wopambana ukubwerawo, chirombo chimene chiti chidzawuke. Chotero, Mpingo ukubwera mwanjira yomweyo, kupyola mu kulungamitsidwa, kuyetsedwa, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi Khristu akukhala mwa anthu, ndendende basi. Ndipo iye ali nacho chotsutsa cha Icho pamwamba apo, a...mwaona, choyimira cha Icho, kani. Ndi uyo pamenepo, ndendende basi. Ndi iyeyo. Waponyedwa kuchokera Kumwamba.

¹⁶⁷ Tsopano ife tikupeza, mu Chivumbulutso 13:1 mpaka 8.

Ndipo ine ndinayimirira pa michenga ya mnyanja, ndipo ndinawona chirombo chikuwuka...

¹⁶⁸ Tsopano, apa ndi pa 12, pamene iye anaponyedwera kunja. Tsopano penyani.

...ndinawona chirombo chikuwuka kuchokera mnyanja, chiri nayo mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi, ndipo pa nyanga zake pali akorona khumi, ndipo pa mutu pake pali dzina la mwano.

Ndipo chirombo chimene ine ndinachiwonacho chinali chonga nyalugwe, ndipo mapazi ake...

169 Oh, ngati ife tikanangokhala nayo nthawi tsopano, ife tikanatenga usiku wonse, pa ziphiphiritso zimenezo pamenepo, ndi kuwonetsa, kuzibweretsa izo molunjika kumene kwa iye kachiwiri. Aliyense, pafupifupi ambiri a inu nonse mukuzidziwa zimenezo, kuchokera ku maphunziro ena.

...anali...mapazi a chimbalangondo, ndipo kamwa yake...kamwa ya mkango: ndipo chinjokacho chinampatsa iye mphamvu,...mpando, ndi...ulamuliro.

170 Huh! Satana mthupi! Mukuona?

Ndipo ine ndinawona umodzi wa mitu yake ngati iwo...unavulazidwa kwa imfa;...

171 Ndipo mpaka mmusi, pamene ife tikupitirira, ngati inu mukufuna kuteri, inu mukadzapeza mwayi wowerenga mpaka mmusi. Ayi, tiyeni—tiyeni tingowerenga pang'ono pokha.

Ndipo ndinawona umodzi wa mitu yake ngati kuti iwo unali utavulazidwa...imfa; ndipo bala lake la ku imfa linapola: ndipo dziko lonse linazizwa ndi chirombocho.

172 Inu mungopenyetsetsa! Inu musamachipenyetsetse chikominisi nkomwe. Icho sikanthu koma chida, chikusewera mmanja mwa Mulungu, kuti chidzakuthandizeni inu tsiku lina kudzapeza, “kudzabwezera magazi,” monga mmene ife titi tidzazipezere izo mawa usiku. Mukuona?

Ndipo iwo anapembedza chinjokacho...

173 Chinjokacho chinali ndani? Satana. Nkulondola uko? “Chinjoka chofiira.” Chabwino.

...chimene chinapereka mphamvu kwa chirombocho (kumene iye amatenga mphamvu yake, mwaona): ndipo iwo anachipembedza chirombocho, kunena, Ndani ali wofanana ndi chirombocho? ndani angakhoze kuchita naye nkondo iye?

Ndipo kunapatsidwa kwa icho kamwa yoyankhulira zinthu zazikulu za mwano; ndipo mphamvu inaperekedwa kwa iye kuti akapitirize kwa miyezi forte ndi thuu.

Ndipo iye anatsegula kamwa yake mwamwano motsutsa Mulungu, (Ndi zimenezotu pamenepo, mwaona. Chabwino)...kuchitira mwano dzina lake, (kumupatsa iye udindo)...kachisi wake (amene ali malo okhalapo Mzimu Woyera),...

174 Kuwapanga iwo kukhala malo a mu Roma, Mzinda wa Vatican. Inu mukhoza kumangopitirira mpaka mmusi:

...ndi iwo akukhala kumwamba.

175 Anawachitira mwano iwo, ponena kuti iwo anali opembedzera.

Ndipo kunapatsidwa kwa iye kuti achite nkondo ndi oyera (ndipo iye anachita), ndi kuti awagonjetse iwo (iye anatero): . . .

176 Anawawotcha iwo pa nkhu! Kuwadyetsa iwo kwa mikango! Ndipo anawapha iwo mwanjira iliyonse yomwe iye akanatha!

. . . ndipo mphamvu inaperekedwa kwa iye pa mitundu yonse, . . . malirime, ndi mafuko.

177 Izo sizinafikipo mwanjira imeneyo mu Roma kufikira pamene Roma wachikunja anatembenuzidwa nkudzakhala Roma wa upapa, ndipo mphamvu ya Chikatolika inafalikira pa dziko lapansi, anapanga mpingo wa Katolika wa konsekonse.

Ndipo onse amene akukhala padziko lapansi adzamupembedza iye, amene maina awo sanalembedwa mu bukhu. . .

178 “Usakhudze Mafuta Anga ndi vinyo!” Mukuona?

Ndipo onse okhala padziko lapansi adzamupembedza iye, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo wa Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi.

Ngati munthu aliyense ali nalo khutu, muloleni iye amve.

Iye amene atsogolera ku ukapolo adzapita ku ukapolo: iye amene apha ndi lupanga ayenera adzaphedwe ndi lupanga. Apa pali chipiriro ndi. . . chikhulupiriro cha oyera.

179 Tsopano, ife tinali naye iye akubwera, usiku wathawu, ndi lupanga lake lalikulu, kuti akaphe.

180 Ife tinapeza kuti iye akudzaphedwa ndi lupanga, nayenso, lupanga la Mawu. Mawu a Mulungu, akuthwa, lupanga lakuthwa konsekonse, lidzamudula iye, lidzamusiya iye pansu pomwe. Dikirani mpaka Mabingu Asanu Ndi Awiri amenewo adzayankhule maliwu Awo kwa gulu limenelo omwe adzakhoze kwenikweni kudzawatenga Mawu a Mulungu ndi kudzawapereka Iwo kumeneko, Iwo adzayengula ndi kudula. Ndipo iwo adzakhoza kutseka miyamba. Iwo akhoza kutseka *ichi*, kapena kuchita *icho*, chirichonse chimene iwo akufuna kudzachita. Ulemelero! Iye adzadulidwa ndi Mawu amene azidzatuluka kuchokera mkamwa Mwake, ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse. Iwo akhoza kudzaitanitsa matani handiredi billioni a ntchentche ngati iwo angafune kutero. Amen. Chirichonse chimene iwo adzanena, chidzachitika, chifukwa Ndiwo Mawu a Mulungu akubwera kuchokera mkamwa mwa Mulungu. Eya. Amen. Mulungu,

nthawizonse, Ndiwo Mawu Ake, koma Iye nthawizonse amamugwiritsa ntchito munthu kuti awagwiritse ntchito Iwo.

¹⁸¹ Mulungu akanakhoza kuyitanitsa ntchentche zija, uko ku Igupto, koma Iye anati, “Mose, iyo ndi ntchito yako. Ine ndingokuwuza iwe choti uchite, ndipo iwe upite ukachichite icho.” Iye anakachita icho mokwanira. Mukuona? Iye—Iye akanakhoza kusankha dzu—dzuwa kuti liyitanitse izo, Iye akanakhoza kupangitsa mwezi kuti uyitanitse izo, kapena mphepo kuti iyitanitse izo. Koma, Iye—Iye anati, “Mose.” Kuti—ndiyo. . . Iye amasankha munthu. Chabwino.

¹⁸² Tsopano ife tinapeza apa, kuti Satana uyu, atatha kuponyedwa kuchokera Kumwamba, anadzikhazikitsa yekha mwa chirombo. Ndipo tsopano iye ndi chirombo; wotsutsakhristu, mneneri wabodza, ndipo tsopano chirombo. Ndipo wapatsidwa dzina la Imfa! Ndipo Gehena ikumutsatira iye! Satana wathunthu, ali pampando wachifumu wake! Oh, mai! Pa dziko lapansi, iye ndi Satana, woyimira, pa dziko lapansi, kuti iye tsopano ndi mutu wa maufumu a m’dziko, maufumu omwewo amene iye anawapereka kwa Ambuye Yesu mu Mateyu 4. Satana tsopano akukhala mfumu yathunthu.

¹⁸³ Tsopano, izi zidzachitika mtsogolo. Iye ndi mneneri wabodza tsopano. Iye adzakhala chirombo, pakapita kanthawi, pamene iye adzaswa pangano lake kumeneko ndi Ayuda. Inu mukudziwa momwe ife. . . Chabwino, zindikirani tsopano, iye adzapatsidwa mtima wa chirombo, pa nthawi imeneyo, ndipo Satana adzadzizika yekha mthupi. Chifukwa, pamene Mpingo ukupita mmwamba, Satana akuponyedwa kunja. Mukuona? Mukuona? Izo zatheka, pamenepo, ndizo, kutsutsa kwake konse kwatha. Mukuona? Tsopano, bola ngati. . .

¹⁸⁴ Taonani, bola ngati Wopembedzera akadali pa Mpandowachifumu, Satana akhoza kuyima pamenepo ndi kumatsutsa, chifukwa iye ndi woyimira mlandu wa mbali inayo. Iye ndi mdani wa Khristu. Ndipo Khristu ndi. . . Iye akuyima pamenepo, a—a—mdaniyo akuyima pamenepo, akuti, “Koma, yembekezani! Adamu anagwa! Adamu anachita *ichi*! Ine ndinamugonjetsa iye. Ine ndinamupangitsa mkazi wake kuti akhulupirire bodza. Ndipo Inu munati iye akanadzawonongedwa nalo ilo. Ine ndinachipeza icho!”

¹⁸⁵ Koma apa pali Mkhlapapakati atayimirira pamenepo, ameni, Muwomboli Wachibale, ameni, ataimirira pamenepo ndi Magazi amene angakhoze kutenga mtima wa wochimwa woyipitsitsa ndi kuwusinthia iwo. Mkhlapapakati ali pa Mpandowachifumu. Inde, bwana.

Satana anati, “Koma iwo ndi olakwa!”

Iye akhoza kunena kuti, “Iwo siali ayi.”

186 Clorox imeneyo inakonzedwa, kapena inapangidwa, kuti idzichotsa banga, kuchotsa kuthimbiritsa kwa inki kapena banga lina lirilonse. Iwo ali nayo iyo. Iyo idzaswa ilo mpaka inu simudzalipeza konse ilo kachiwiri. Ilo limabwerera ku mipweya, ndi njira yonse kubwerera ku kuwala kwa dziko. Ndipo limapitirira mamolekyulu ndi china chirichonse, mpaka ilo limabwerera kuchiyambi kumene ilo linachokerako. Ichu ndi chirengedwe. Chinkayenera . . . Chirengedwe, ichu chinkayenera kubwera kuchokera kwa Mlengi. Koma mankhwala onse amene anapangidwa ndi kuikidwa pamodzi, iwo amaswedwa, ndipo ndizo basi zonse zomwe ziripo kwa ilo. Palibe zinanso za ilo. Ngakhale limene—thunthu kumene la madzi lomwe liri, limagwirizana ndi Clorox, amene ali mapulusa.

187 Amen! Ulemelero kwa Mulungu! Zonse ndi zoyera. Ndicho chimene Magazi a Yesu Khristu amachita kwa mwana wona wa Mulungu, pamene iye avomereza tchimo limenelo ndi kuyima pamenepo, wolungamitsidwa mu Chake . . . Chifundo! Kalanga! Izo ndithudi ndi zazikulu kwambiri mpaka Mulungu anati, “Ine sindingakhoze ngakhale kulikumbukiranso ilo nkomwe. Ndipo iye ali mwamtheradi mwana Wanga.”

188 “Indetu, Ine ndinena kwa inu, ngati inu mudzanena kwa phiri ili ‘suntha,’ ndipo osakayikira mu mtima mwanu, koma kukhulupirira mu chimene inu mwanena, inu . . . chidzachitika. Inu mukhoza kukhala nacho ichu chimene inu mwanena kuti chikhalapo.” Inu ndinu mwana wowomboledwa. Amen! Ine ndikudziwa kuti izo nzoona.

189 Ine ndawonapo agologolo akuwonekera kutsidyako, pa nthawi sikisi zosiyanasiana, zomwe ine ndimazidziwa, ndipo osatinso kuposa omwe angadzakhale pano. Iye ali basi monga . . . Iye akhoza kulenga agologolo mofanana ndi momwe Iye angakhazere kulenga ntchentche, kapena achule, kapena china chirichonse. Iye, Iye ndi Mulungu, Mlengi. Kulondola! Ndipo pamene palibe munthu wachivundi . . .

190 Koma pamene tchimo lija la chivundi ilo lalapidwa ndi kugwetseredwa mu Clorox imeneyo, ya bulitchi ya Yesu Khristu, Iyo imachotsa tchimo lonse. Iye amakhala wosakhudgidwa mwangwiro, wopanda tchimo, wopanda cholakwika. “Iye amene ali wobadwa mwa Mulungu samachita tchimo, pakuti iye sangakhaze kuchimwa.” Bulitchiyo imayima pakati pa iye ndi Mulungu. Lingakhaze bwanji ilo nkomwe kukafika pamenepo, pamene iyo imaliswa ilo ndi kulumiza ilo kumbuyo kumene kwa iye amene analipotoza ilo! Amen!

191 Psyii! Ine ndikumverera mwachipembedzo. Ine—ine ndikukuuzani inu, ine ndikukondowezeka tsopano pamene izi zikuyamba kuwululidwa.

192 Zindikirani, Satana kwathunthu, ali pa mpandowachifumu wake. Inde, bwana. Anawupereka iwo kwa Mulungu,

anawupereka iwo kwa Ambuye wathu. Apa iye ali, wakhala apa, ali ndi mtima wauchirombo uwu mwa iye. Tsopano, apa pali munthuyo, chirombo, mdierekezi mthupi. Iye akupanga kuwonekera kwake apa pa dziko lapansi, mwa kunyengezera kwabodza. Oh, mai, kalanga! Pansi pa kunyengezera kwabodza kwa Mawu owona, iye akudziyanjanitsa yekha ndi Mawu.

¹⁹³ Iye anachita basi chinthu chomwecho chimene wake—womuyimira wake anachita, amene anali Yudas, zaka thuu sauzande zapitazo. Kodi iye anachita chiyani? Yudas anadalowamo, ngati wokhulupirira, pokhala mdierekezi kuchokera pachiyambi. “Iye anabadwa ali mwana wachitayiko.” Iye sanakokere kanthu pa Yesu, chifukwa Iye ankamudziwa iye kuchokera kuchiyambi komwe; ameni, pakuti Iye anali Mawu. Chabwino. Ndipo, kumbukirani, Yudas anatenga malo monga msungichuma, ndipo anagwetsedwa ndi ndalama.

¹⁹⁴ Momwemonso ukutero mpingo wa tsiku lino! Mpingo wa Katolika, monga ife tinazindikirira usiku wathawu, kulipiritsa kupembedzera, kulipiritsa mapemphero, ndi kulipiritsa chirichonse. Ziri pafupifupi chimodzimodzi, ndipo ana aakazi a mpingo wa Katolika anagwa pa chinthu chomwecho, anachitira Achiprotetanti. Chinthu chonsecho chakutiridwa mu ndalama. Apo ndi pamene Yudas anagwera, ndipo apa ndi pamene iye anagwera, ndipo apo ndi pamene Achiprotetanti akugwera.

¹⁹⁵ Penyani, akukwera kavalo wotumbululuka pamene iye akuwonekera pa kukwera kwake, kukwera kotsiriza uku. Iye ali pa wotsiriza wake tsopano. Tsopano, izo siziri mu tsiku lathu. Izo zidzakhala kumusi uko. Ndi Chisindikizo, choloseredwa. Chifukwa, mwaona, Mpingo udzakhala utapita kale pamene izi zidzachitika. Pamene Khristu adzawonekera kuno pa dziko lapansi, monga—monga—monga. . . Munthu uyu akuwonekera, ndipo akudzakhala kwathunthu, mdierekezi wathunthu; kuchokera kokhala wotsutsakhristu, njira yonse mpaka mmusi, kudutsa mwa mneneri wabodza, kenako mpaka mwa chirombo, mdierekezi mwiniwake. Ndipo iye akukwera pa kavalo wotumbululuka, wamitundumitundu yonse, ndi wosakanizidwa ndi mitundu yonse yosiyanasiyana, kuti imupange iye kukhala wotumbululuka ndi wakupha.

¹⁹⁶ Koma pamene Ambuye wathu adzawonekera kuno pa dziko lapansi, Iye adzakhala atakwera pa kavalo woyera ngati chipale. Ndipo Iye adzakhala kwathunthu, wokwanira, Emanuele, Mawu a Mulungu mthupi la Munthu. Mukuona? Ndiko basi kuchuluka kwake kwa kusiyana komwe kulipo mwa iwo. Ndiko kusiyana kwake kwa iwo.

¹⁹⁷ Zindikirani, wotsutsakhristu ali pa kavalo wotumbululuka, wosakanizika mitundu. Kavalo ndi chirombo chimene chimayimira mphamvu. Mphamvu yake yonse ndi yosakanizika. Chifukwa chiyani? Pali ndale, pali—pali mphamvu za fuko,

pali mphamvu za chipembedzo, pali mphamvu za ziwanda. Ndizo mphamvu za mitundu yonse itasakanizidwa pamodzi, itasakanizidwa, anali kavalo wotumbululuka. Iye ali nazo mphamvu za mitundu yonse.

¹⁹⁸ Koma pamene Yesu adzabwera, adzakhala ali pa kavalo wamtundu umodzi wokhazikika, Mawu. Amen!

¹⁹⁹ Uyu akusakaniza mitundu yake, wofiira, woyera, wakuda; mitundu itatu mwa mmodzi, itaimiridwa mwa mmodzi. Ndipo mphamvu zitatu zikuimiridwa mwa mmodzi; kavalo woyera, kavalo wakuda, kavalo wofiira. Ndi akorona atatu, mwa mmodzi. Mukuona? Ndithudi.

²⁰⁰ Ine ndinamuwona koronayo, inemwini; ndinayima, oh, pafupi *chotero* ndipo ndinayang'ana pa iye. Sakanandilola kuti ndifikire kwa iye, pa chifukwa cha galasi, pa iye. Kotero uyo anali pamenepo, loko wamkulu pa iye, atakhala mu chikwama: korona wa patatu. Kotero ine ndikudziwa kuti ndi choonadi. Uh-huh. Kotero iye anali pamenepo, korona wa patatu, vicar: kumwamba, purigatorio, ndi dziko lapansi.

²⁰¹ Mphamvu zitatu zitalumikizana pamodzi, mwaona, zonse zitasakanizika mu mtundu, wotumbululuka. Imfa inayankhula mu chinthu chonsecho; zandale, ndi—ndi zachipembedzo, ndi—ndi mphamvu za ziwanda, zitasakanizika pamodzi. Ndale, iye ndi mfumu ya ndale, Satana ali. Wanzeru! Psyii! Ndithudi. Musayesetse kumuposa iye. Ingo—ingodalirani pa Ambuye. Ndizo zonse.

²⁰² Monga ndakhala ndikunenera, zonse, tinadutsamo kale. Anzeru onse, zamaphunziro ndi zinthu monga izo, zimabwera kuchokera ku mbali yolakwika. Ingozitsatirani izo kudutsa mu Lemba, mupeze ngati izo ziri zolondola. Muwatsatire ana a Kaini ndipo muwone chimene iwo anadzakhala. Kenako muwatsatire ana a Seti, muwone chimene iwo anali. Osati kuti ndikuthandizira umbuli, ayi nkomwe. Ayi, bwana. Koma mumutenge munthu aliyense, nkomwe, wa m'Baibulo, patalipatali kwambiri. . .

²⁰³ Ndipo pali mmodzi wotchedwa Paulo, yemwe anali munthu wophunzira, ndipo iye anati iye ankayenera kuiwala chirichonse chimene iye ankachidziwa, ndi cholinga chakuti amudziwe Khristu. Iye anati, “Ine sindinabwere kwa inu ndi mawu odolola a nzeru za anthu, koma ine ndabwera kwa inu mu Mphamvu ya chiwukitsiro cha Khristu.” Uko nkulondola, Mphamvu ya Mzimu Woyera!

²⁰⁴ Tayang'anani pa enawo. Ena a iwo sankadziwa ngakhale kusiyantsa dzanja lamanja ndi la manzere. Ndipo—ndipo, oh, tayang'anani mmusi kudutsa mu m'badwo wa aneneri, ndi kumene iwo ankachokera, ndi zina zotero. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

²⁰⁵ Mwaona, ndi ophunzira, aluntha, ndi anzeru. Nzeru ndi ndendende chinthu chomwecho chimene chimakutengera iwe kutali ndi Mulungu.

²⁰⁶ Iye anali ndi mphamvu zitatu, kapena atatu—maulamuliro atatu: dziko lapansi, Kumwamba, ndi purigatoriyo.

²⁰⁷ Iye ali, mwiniwakeyo, utatu. Ndicho mapangidwe a iye. Ndipo iye akukwera mu utatu. Mphamvu yake ili mu utatu. Korona wake ali mu utatu. Kavalo wake ali mu utatu. Ndi chimene iye ali, utatu; mphamvu ya utatu, korona wa utatu, kavalo (akukwera) wa utatu; ndiwo maudindo, zinayi kenanso, mwaona, zinayi kenanso. Chabwino.

²⁰⁸ Magawo atatu a utumiki wake, akumupanga iye kukhala munthu mmodzi, Satana mthupi. Magawo atatu a utum-... wotsutsakhristu, mneneri wabodza, ndi chirombo. Zitatu zimenezo, zikuyimira, mwaona. Tsopano apo pali zoyimira zitatu, tsopano, apo zikumupanga iye.

²⁰⁹ Mulungu, Mulungu amadzidziwitsa Yekha, nayenso, mwa madzi, Magazi, Mzimu; zimamupanga Mkhristu kukhala mwana wa Mulungu, mwa Mawu a Mulungu. Mukuona? Ndipo mphamvu zitatu *izi* zimamupanga iye kukhala mdierekezi. Mukuona? Oh, Izi apa, ndi madzi, Magazi, ndi Mzimu, zomwe ziri za Mulungu. Ndipo *izo* ndi ndale, chipembedzo, ndi mphamvu ya ziwanda, zitasakanizika pamodzi, zikumupanga iye kukhala mdierekezi.

²¹⁰ Kudza koyamba kwa Khristu, wachivundi. Iye akubwera nthawi zitatu. Khristu ali mu zitatu. Mukuona? (Penyani momwe iye akubwerera; iye ali panayi.) Mpenyeni Khristu. Kudza Koyamba, Iye anabwera wachivundi, kudzakhetsa magari ndi kufa. Nkulondola uko? Ndiko kudza Kwake koyamba. Kudza Kwachiwiri ndi Mkwatulo; ife tidzakomana naye Iye mu mlengalenga, wachisavundi. Kubwera Kwake kwachitatu, Iye ali Mulungu mthupi. Amen! Mulungu, Emanuele, kuti adzalamulire pa dziko lapansi! Uko nkulondola, katatu kokha.

²¹¹ Gawo lachinayi la wokwerayu, yang'anani. Gawo lachinayi la wokwera uyu likutchedwa Imfa. *Imfa* imatanthauza “Kulekana kwamuyaya ndi Mulungu.” Ndicho chimene imfa imatanthauza, kukhala wolekanitsidwa Kwamuyaya ndi Mulungu.

²¹² Tsopano, ngati ife tamuyika munthu uyu panja, ophunzira, ngati ife tawonetsera mwa Baibulo, yemwe munthu ameneyo ali; ndipo ife tinatenga ngakhale mapiri, malo ndi paliponse, ndendende basi mwa tsatanetsatane, kupitirira mpaka mmusi. Ndipo tsopano iye akutchedwa, ndi mphungu, “Imfa.” Ndicho chimene Iye akumutcha iye. Kumbukirani, apa, mwaona, imfa ndi kulekana Kwamuyaya.

²¹³ Kumbukirani, oyeri samafa. Iwo amagona, osati kufa. “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene

anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya.” Uko nkulondola. “Sadzafika mu chiweruzo; wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Ine ndine Chiwukitsiro ndi Moyo,” anatero Yesu. “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye atafa, komabe iye adzakhala ndi moyo. Ndipo aliyense amene akhala moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse.” Lazaro, wafa? “Iye akugona.”

²¹⁴ “Musawope ayi, mtsikanayu sanafe, koma akugona.” Iwo anamuseka Iye monyogodola. Nkulondola uko? Oh, mai! Mwaona, oyera samafa.

²¹⁵ Kulekana ndi Mulungu ndiyo imfa, imfa Yamuyaya. Ndipo munthu uyu akutchedwa “Imfa,” kotero muzikhala kutali ndi iye. Kodi iye ndi ndani? Kachitidwe kachipembedzo, kabungwe; woyamba, mpingo, woyamba, kuchita bungwe, ndipo pamene iye anatenga—kumvetsa kwa Konstantine, pa Msonkhano wa Nicaea.

²¹⁶ Iye tinawabweretsa akazi amenewo, usiku watha, ndi kuwonetsa momwe Eva, mkwatibwi woyamba, mwamuna wake asanafike konse kwa iye, iye anagwa, pa kusakhulupirira Mawu a Mulungu mu Edeni. Mkwatibwi wauzimu wa Khristu amene anabadwa pa Tsiku la Pentekoste, Iye asanafike kwa mkaziyo, chinachitika ndi chiyani? Iye anagwa, ku Roma. Chiyani? analanditsa ukoma wake wa Mawu, pofuna mbalume. Amen. Oh, mai!

²¹⁷ Ine—ine—ine ndikumverera kukondoweza kukubwera pa ine kachiwiri, inde, bwana, ndikamaganiza za zimenezo... Ine sindikutanthauza kuti ndichite mopenga. Ine sindikutanthauza zimenezo. Koma ine basi... Inu simukuzindikira chomwe izo zimachita kwa ine. Ine ndakhala ndiri mu izi kwa masiku anayi tsopano. Basi...ndipo ine ndimangoyenera kuyankhula chinachake, kuti ndikhale ngati ndayamba kumverera mwa umunthu kachiwiri. Inu mukudziwa chomwe ine ndikutanthauza. Eya. Chabwino. Ukayamba kuyankhula monga choncho, ndipo iwe umawona masomphenya akufalikira pamalo ponsepo. Uko nkulondola. Mwaona, ndi chifukwa chake ine ndimayankhula chinachake kuti ndizibweze ndekha kachiwiri, ndi kudzigwedezanso kachiwiri. Mukuona?

²¹⁸ Kodi inu munayamba mwandizindikirapo ine pamene ndikukhala ndi mzere wa kuzindikira za mumtima? Ine ndimanena chinachake, chimene chiwapangitse anthu kuseka; kenako ine ndimadzanena chinachake, chowapangitsa anthu kulira; kenako ndimanena chinachake, chowapangitsa iwo kukwiya. Ine ndimapeza chinachake chitawonekera. Ndipo ndimanena chinachake, kuti ndiwone momwe icho chingalandiridwire, ndikatero ndimawona mtundu wa kuwala kumene kuli pa iwo, chimene chikuchitika. Zikatero ine ndimadziwa pamene icho chiri, ndipo ine ndimadziwa ngati

Icho chikuitana kapena ayi. Ngati icho si chimenecho... Amakhala pamenepo, wokhulupirira weniweni, chabwino. Iwe umawayitana iwo, pamenepo, kuti, “Inu, *Akuti-ndi-akuti*.” Mwaona.

²¹⁹ Ndipo pamene iwe ufika kumeneko, Mzimu umayamba kudzoza, kenako umayamba kuwona kuthwanima uko kukubwera paliponse, mwaona, monga chomwecho, kumazungulira, kumazungulira mchipindamo. Kotero, ndi chifukwa chake ine ndimanena chinachake, kuti ndikhale ngati ndikuyambiranso mmbuyo kachiwiri, kuyambiranso mwatsopano kachiwiri, mwaona.

²²⁰ Kuyambira Lamlungu latha, ine ndikumangokhala mchipinda momwe, kumangopemphera, ndizo zonse, ndipo pansi pa kudzoza. Ndipo ine ndikudziwa kuti Izi nzoona. Ngati inu mukukhulupirira Mulungu, ine ndikudziwa kuti inu mukutero, inu mungoyang’ana pakutha pa sabatayi. Uh-huh. Mukuona? Mukuona? Chabwino. Mukuona?

²²¹ Tsopano, imfa imatanthauza kulekanitsidwa Kwamuyaya ndi Mulungu. Ndipo kumbukirani, tsopano, overa samafa.

²²² Kumbukirani, mkwatibwi wake anapatsidwa kavalo wotumbululuka, a...ine ndikutanthauza, wokwera uyu anapatsidwa kavalo wotumbululuka, kuti—kuti azipita naye. Iye anapatsidwa uyu—kavalo wotumbululuka uyu, kuti azipita naye. Ndipo iye anakwera kavalo wotumbululuka uyu, wa imfa. Tsopano ife tikudziwa chomwe icho chinali. Ife tikudziwa umene mpingo wake unali.

²²³ Ndipo kumbukirani, mu usiku watha, iye sanali kokha “hule,” iye anali “mayi wa timahule.”

²²⁴ Ndipo ife tinapeza, kuti chimene chinamupanga iye kukhala hule, chinali, mkazi amene ali wa mtundu umenewo. Ndine basi...Ndi mawu osanyengerera, kuwayankhula pakati pa gulu losakanikirana. Koma Baibulo limanena zimenezo, mukuona. Kotero, ndiye, ife tikuzindikira kuti ndiye—ameneyo ndi mkazi amene amakhala moyo wosawona kwa malumbiro ake achikwati. Ndipo inu mukuona, iye akuyenera kukhala chomwecho, amanena iyemwini, amadzitcha yekha, “Mfumukazi ya Kumwamba.” (Ameneyo angakhale Mkwatibwi wa Mulungu. Mulungu ndi Khristu.) Ndipo ife tikupeza kuti iye akuchita ziwerewere, ndipo iye akuwapangitsa mafumu a dziko lapansi kuchita ziwerewere, ndi anthu onse olemera, ndi anthu opambana. Dziko lapansi lonse linamutsatira iye. Mukuona?

²²⁵ Ndiyeno ife tinapeza kuti iye anabereka ana ena aakazi, ndipo iwo anali timahule. Kodi kahule ndi chiyani koma hule, chinthu chomwe chomwecho; wachiwerewere, ziwerewere, zoipa, zigololo, kumazichita. Kodi iwo anachita chiyani? Anapanga bungwe, anatenga kachitidwe, anaphunzitsa zopangidwa ndi munthu, Pentekoste ndi gulu lonselo!

226 Tsopano, musalole chanu—chikumbumtima chanu chigwere mu thumba lanu, Pentekoste. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Tiyeni tichiyang'ane chinthucho mu nkhope momwe. Ife tachedwa kwambiri panjirayi tsopano, kuti tizipita tikubweza nkhonya. Yang'anani apa.

227 Ife tikukhala mu M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Ndipo umenewo unali m'badwo wa mpingo wopusa kwambiri mwa ina yonseyo, wofunda, ndipo umodzi wokhawo umene Khristu anali kunja, akuyesetsa kuti abwerere mkati. Ndipo ndiwo uthenga wa Chipentekoste ukupita, unati, “Ndine wolemera!” Mnyamata, iwe unali wosauka, poyamba. Tsopano iwe wakhali wolemera, mwaona. “Sindisowa kanthu!” Ndipo—ndipo, oh, chomwe iwe unali!

228 Iye anati, “Ndiwe wamaliseche, womvetsa chisoni, wakhungu, wosauka, watsoka, ndipo sukudziwa konse zimenezo.”

229 Tsopano, ngati munthu atakhala wamaliseche, kunja uko pa msewu, ndipo nkumadziwa zimenezo, bwanji, iye angayesetse kudzithandiza yekha. Koma pamene iye—pamene iye sakudziwa zimenezo, ndipo iwe sungakhoze kumuuzwa iye kusiyana kulikonse, ndiye iye ali mu chikhaliidwe choipa. Mulungu amuchitire iye chifundo. Kulondola. Zindikirani. Oh, mai!

230 Tsopano, kumbukirani, wotsutsakhristu uyu, iyemwini, pokhala mwamuna; mkwatibwi wake, umene uli mpingo wake, “anapatsidwa danga kuti alape, ndipo iye sanachite zimenezo,” mu m'badwo wa mpingo umenewo, Tiyatira. Inu mukukumbukira zimenezo? Mungakhoze inu. . . ?

231 Chabwino, tiyeni tibwerere mmbuyo miniti chabe. Sizitipweteka ife kubwerera mmbuyo kwa miniti yokha. Tiyeni tibwerere mmbuyo, kwa mutu wa 2, miniti yokha. Ife tingowerenga izo, mutu wa 2 wa. . . tsopano, Tiyatira. Tsopano penyani ichi, basi mwamsanga kumene tsopano. Mai, ife tayandikira nthawi yoti tizitseka, ndipo sitinayambe. Koma, zindikirani, Tiyatira. Tsopano, izo zikuyambira pa ndime ya 18 ya a—mutu wa 2.

. . . kwa mngelo (ndiye mtumiki) wa mpingo mu Tiyatira lemba; Zinthu izi anena Mwana wa Mulungu, amene ali nawo maso ake onga malawi. . . ndi mapazi ake ofanana ndi mkuwa wonyezimira;

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi chikondi chako, ndi utumiki wako, ndi chikhulupiro chako, . . . chipiro chako, ndi ntchito; ndipo iwe uyenera kukhala mochuluka kuposa. . . ndipo zotsiriza ziyenera kukhala mochuluka kuposa zoyamba.

Komabe ine ndiri nazo zinthu pang'ono zokutsutsa iwe, chifukwa iwe ukumulola mkazi uja Yezebeli, . . .

232 Ndi zimenezotu pamenepo. Inu mukumudziwa iye, mu Baibulo. Iye anali mkazi wa Ahabu. Ndipo apa pali mkazi, mpingo, Yezebeli, mkazi wa mneneri wabodza, amene amayenera kukhala mneneri weniweni wa Mulungu, papa; kulondola, mneneri weniweni ndi mkazi wake, Yezebeli. Tsopano, Ahabu ankayenera kukhala Myuda weniweni, koma iye anali mthakati, inu mukudziwa zimenezo, chifukwa mkazi wake ankangomutsogolera iye mwanjira iliyonse imene iye angafune kutero. Ife tikupeza kuti, Yezebeli akutenga ndalama zake ndi kuwatsogolera awa mwanjira yomwe iye akufunira kutero, nayenso.

...yemwe amadzitcha yekha mneneri wamkazi, (mukumvetsa zimenezo?), kuti akaphunzitse ndi... kuwalamulira antchito anga (mwaona, chiphunzitsa icho cha Yezebeli chinangosesa dzikolo) kuti akachite ziwerewere ndi... kudya zinthu zoperekedwa nsembe kwa mafano.

...Ine ndinampatsa iye danga kuti alape (mukuona?) za ziwerewere zake; ndipo iye sanalape ayi.

233 Yang'anani ndime yotsatira iyi.

...Ine ndidzamponyera iye pa kama (ndiyo gehena), ndi iwo amene anachita naye iye chigololo kuwalowetsa ku zisautso zazikulu, ... (Ndiko kukalowa mu Chisautso chachikulu. Osati Mpingo, tsopano.)... pokhapokha iwo atalapa zintchito zawo.

234 Tsopano yang'anitsitsani, apa.

...Ine ndidzawapha ana ake (timahule take) ndi imfa (imfa yauzimu);...

235 Inu mukukhulupirira zimenezo? Amenewo ndi Mawu. "Ine ndidzawapha iwo ndi imfa." Ndipo ngati iwo aphedwa, iwo alekanitsidwa Kwamuyaya. Chabwino. Kumbukirani, Iye anamupatsa iye danga kuti alape.

236 M'badwo wa Tiyatira unali m'badwo wa mdima. Wokwera pakavalo wakuda ankakwera mu nthawi imeneyo, pamene misa zonse ndi chirichonse zinkayenera kulipiridwa, ndi mapemphero, ndi—ndi mapembezidzero, ndi zina zotero. Tsopano onani kavalo wake wakuda, ndiye, iye atatha kukana kulapa mu Tiyatira, (chiyani?) akusintha kukwera kwake kuchoka pa kavalo wakuda nkupita pa wotumbululuka, imfa, kwa utumiki wake wotsiriza.

237 Tsopano, ine ndikhoza kungomupatsa winawake kugwedeza pang'ono apa. Kumukana Mulungu, kukana kuitana kwa Mulungu, inu mudzachita izo nthawi yotsiriza nthawiyina. Ndipo, basi monga momwe mpingo uja unachitira, iwo unatha. Chipiro, cha Mulungu, sichidzalimbana ndi munthu nthawizonse. Mukuona?

²³⁸ Ndipo pamene iye anawakana Iwo, ndi kukana kuwalandira Iwo, ndiye iye anasintha ndi kupita . . . Ndipo tsopano iye ali nalo dzina lotchedwa “Imfa,” kulekanitsidwa. Mulungu anati, “Ine ndidzatenga ngakhale ana ake, Achiprotestanti, ndi aliyense wa iwo Ine ndidzamupha ndi kulekanitsidwa Kwamuyaya.” Ndi zimenezotu, M’badwo wa Tiyatira, m’badwo wa mdima. Kavalo wake wakuda tsopano akutembenukira ku imfa, kwa utumiki wake wotsiriza.

²³⁹ Mukuona momwe mibadwo ya mpingo ikulumikizirana ndi Zisindikizo? Mwangwiro basi. Ndipo ife tikudziwa kuti Izo ndi zoon. Mzimu Woyera sumalakwitsa. Iye anatipatsa ife chitsimikiziro chachikulu, nthawi yapitayo, pamene tinkatsirizitsa mibadwo ya mpingo iyi kumbuyo uko, inu mukudziwa.

²⁴⁰ Mukuona kukondako, kupirira kotalika kwa Mulungu! Iye asanapereke chiweruzo pa iye, Iye anamupatsa iye malo kuti alape. Ndipo ndi mu Dzina la Ambuye ine ndikunena izi: Iye wawupatsa mpingo wa Chiprotestanti chinthu chomwecho, ndipo iwo suchita zimenezo. Uthenga wagwedeza konsekonse, ndipo iye sachita zimenezo. Iye akhalabe nazo mbalume zake ndi tizikhulupiriro, ine sindikusamala kaya inu muzilongosola chotani Zimenezo.

²⁴¹ Monga ine ndinanena uko mu Chicago, tsiku lina, pamaso pa atumiki ambiri kuposa momwe anthu akhalira pano! Ndipo kumeneko iwo anandipanikiza ine, pa Chiphunzitso, cha mbewu ya serpenti ndi chinthu china chonse ichi. Ine ndinati, “Winawake atenge Baibulo lake, ndipo abwere apa ndi kudzayima pambali pa ine ndiye.” Ndipo palibe aliyense ananena kanthu.

²⁴² Tommy Hicks anati, “Ine—ine sindinamvepo Izo monga choncho mmbuyomo, M’bale Branham. Ine ndikufuna firii handiredi a matepi amenewo. Ine ndikawatumiza iwo kwa atumiki anga onse.”

²⁴³ Pamenepo panali pafupifupi fifite, kapena sevente-faivi, anati, “Ine ndikubwera kumeneko kudzabatizidwanso.” Kodi iwo anabwera? Palibe mmodzi wa iwo. Chifukwa chiyani? Iye anawapatsa iwo danga kuti alape! Ndipo Iye adzawaponyera ana anu ku imfa, imfa yauzimu.

²⁴⁴ Ife tidzazitenga zimenezo mawa usiku, Ambuye akalola, kapena Loweruka usiku, pa Miliri imeneyo imene ikudutsako. Inu mudzawone zimene zikudzachitika kumeneko.

²⁴⁵ Monga Iye anampatsira Igupto, Iye anampatsa Igupto malo kuti alape. Ndipo kodi mliri wotsiriza uja unali chiyani? Unali imfa.

²⁴⁶ Ndiwo mliri wotsiriza umene wakantha mpingo wa Chipentekoste, ndi imfa yauzimu. Iwo wafa. Izo ndi mu Dzina la Ambuye. Iwo wafa mwauzimu. Iye awupatsa iwo malo

akuti ulape, ndipo iwo unawakana Iwo. Tsopano iwo wafa. Iwo sudzawukanso konse kachiwiri.

²⁴⁷ Ndipo anthu amenewo kunja uko, akuyesetsa kulowetsamo ma Episcopalia ndi anseme, ndi ena otero, ndi kumawatcha iwo, “Atate Woyera *Wakuti-ndi-wakuti*.” Bwanji, iwo ayenera kudzychitira manyazi okha. Munthu angakhale wakhungu chotani! Kodi Yesu sanatero? Pamene namwali wogonayo anabwera kuti adzagule Mafuta, iye sanawapeze Iwo!

²⁴⁸ Aliyense, inu mumawamva anthu akuti, “Ine ndiri nawo Mzimu Woyera. Ine ndinayankhula mmalirime.” Koma iwo samafuna kubwera pafupi ndi tchalitchi chonga ichi. “Oh, inu mukudziwa, ine sindikukhulupirira ine ndikufuna kumapita pafupi ndi malo ngati amenewo.” Ndiyeno nkumati inu muli nawo Mzimu Woyera?

²⁴⁹ Koma inu mukufuna njira zanu zolemekezeka. Inu mukufuna kumakhala mu Babulo ndipo nkumasangalalabe ndi madalitso a Kumwamba. Inu muyenera kupanga kusankha kwanu. Inu simungamakhale kunja uko mu dziko ndi kumamutumikira Mulungu pa nthawi yomweyo. Yesu anati inu simungakhoze kumutumikira Mulungu ndi mamoni. Koterongati inu simungayembekezere. . .

²⁵⁰ Ngati iwe wapulumutsidwa kwenikweni, iwe udzasangalalana nayo misonkhano imene Mzimu Woyera ukudzitsimikizira Wokha ndi kuwonetsera kuti Mawu a Mulungu ali chomwecho.

²⁵¹ Winawake anati, “Anthuwo amasokosera kwambiri. Zimenezo zimandipangitsa ine manjenje.” Iwe udzakhalawamanjenje ngati iwe uti udzakafike Kumwamba. Ndipo iwe ungoganiza, pamene iwo onse adzakakhala kumeneko, ndiye nanga bwanji zimenezo? Oh, mai! Momwe Ambuye akufunira kutenga. . .

²⁵² Iye ndi wopirira motalika, monga Iye anachitira mmasiku a Nowa. Iye anayesetsa mwamphamvu. Iye anapirira nthawi yaitali, kwa zaka handiredi ndi twente, kuti awafikitse iwo ku kulapa. Iwo sanachite zimenezo.

²⁵³ Mmasiku a Igupto, Iye anatumiza miliri ndi china chirichonse. Iwo sanachite zimenezo.

Iye anamutumiza Yohane. Iwo sanabwerere.

²⁵⁴ Iye anatumiza Yesu, kuti adzafe, kudzapulumutsa gulu lonse limene likanadzamva Mawu.

²⁵⁵ Ndipo tsopano, mmasiku otsiriza, Iye analonjeza kachiwiri kuti Iye akanadzatumiza Uthenga kuti udzamuyitanire Iye kunja, ndi kudzabwezeretsa Chikhulupiriro chapachiyambi kubwerera kwa Iwo, kubwerera ku Mawu. Ndipo iwo sawalandira Iwo. Iwo ndi a mbalume kwambiri, mu mbalume zawo ndi tizikhulupiriro, mpaka iwo sakuwafuna Iwo. Oh, iwo amaganiza kuti ngati iwo akanakhala. . . ngati Mngelo

akanayenda nkudzatsika pansi; koma Mulungu samachita zimenezo.

256 Iye amatenga chinachake chaumbuli ndi chopusa, chinachake chimene sichimadziwa nkomwe ma ABC anu kapena—kapena chirichonse. Ndiyeno Iye amamutenga munthu wa mtundu umenewo, chifukwa Iye akhoza kutenga chinachake chimene chisali kanthu ndipo kenako nkugwira ntchito kupyolera mu chimenecho. Malingana ngati chinachake chikuganiza kuti icho ndi chinachake, ndiye Iye sangachite nacho kanthu icho. Iye nthawizonse wakhala akuchita zimenezo. Iwe umayenera kusakhala kanthu, kuti ukhale winawake ndi Mulungu. Oh, mai!

257 Zindikirani, komabe, “Iye anamupatsa iye danga kuti alape, koma iye sanachite zimenezo.”

258 Iye wachitanso izo kachiwiri; iye sachita zimenezo. Kukana kwake, njira, kukumupanga iye, kapena, kukana kwake kukupanga njira yangwiro kuti Satana abwere mwa iye ndi kudzakhalala mthupi. Uko nkulondola. Kudzadzikhazikitsa yekha mthupi momwe mwa iye, chifukwa iye anawakana Mawu. Ndipo ndicho ndendende chinthu chomwecho chimene mpingo wa Chiprotestanti ukukhala, kahule, ndi chifukwa chakuti iwo ukukana Choonadi chotsimikiziridwa cha Mawu a Mulungu, ndipo icho chikumupatsa mdierekezi malo woti adzalowere mkati momwe ndi kudzadzikhazikitsa yekha mthupi. Ndipo iye adzapanga fano kwa chirombo pamene iwo adzagwirizana pamodzi, kutsidya uko tsopano, ndipo zikungopita momwemo basi momwe Iye ananenera. Uko nkulondola. Amen.

259 Ngati ine ndikanakhala ndi maphunziro, ine ndikanakhocha kuwatulutsa Iwo. Ine ndiribe maphunziro. Ine ndikungoyembekezera kuti Mzimu Woyera uziwululire Izo kwa inu. Ndipo Iye adzatero, kwa iwo amene. . . Uko nkulondola. Iye adzachita zimenezo. Inde. Zindikirani.

260 Yang’anani momwe, chimene iye anachita apa. Iye anakana Uthenga wa Mulungu kuti iye alape. Iye anayambapo, monga wotsutsakhristu, ndipo ndicho chimene iye anali. Iye anabwera, monga mneneri wabodza, mdierekezi mthupi, ndipo, pamene iye anatero, ndi kuphunzitsa kwake kwabodza. Ndipo kenako, mu zonse zimenezo, Mulungu anamupatsa iye danga kuti alape, anayetsa kuti amutenge iye.

261 Mukuona kupirira kotalika kwake? Ndi chikondi chodabwitsa bwanji! Palibe chikondi chonga chimenecho! Tayang’anani pa iwo, ngakhale iwo amene analavulira mu nkhope Yake ndi zinthu, Iye anawakhululukira iwo. Ameneyo ndi Mulungu, mwaona. Musati. . .

262 Anakana Uthenga wa Mulungu! Tayang’anani, iye anapemphedwa kuti alape, kubwerera kumene iye anagwera.

²⁶³ Ndipo kodi iye anagwa kuchokera ku chiyani? Mawu. Kulondola. Eva anagwa kuchokera ku chiyani? [Osonkhana akuti, “Mawu.”—Mkonzi]. Mawu! Chipembedzo chinagwa kuchokera ku chiyani? [“Mawu.”] Ndi zimenezotu pamenepo. Mukuona? Palibe njira ina. Basi, nthawi iliyonse, zikubwerera kumene ku Mawu, kubwerera kumene ku Mawu. Mukuona? Ndipo iwo akulowa mu kachitidwe kamene kakuwachotsa iwo ku Mawu, kakuwachotsa iwo kuchoka ku Mawu mmalo mopita ku Mawu. Zindikirani.

²⁶⁴ Penyani, iye anapatsidwa danga kuti alape, abwerere. *Kulapa* kumatanthauza “kubwerera, kutembenuka, chankhope.” *Lapani*, “bwererani.” Ndipo iye anapatsidwa danga kuti abwerere kumene icho. . .

²⁶⁵ Tsopano kumbukirani, iye anali Mpingo wa chipentekoste, wapachiyambi umene Mzimu Woyera unatsanuliridwapo, pa Tsiku la Pentekoste. Ndi angati ophunzira Baibulo amadziwa zimenezo? Ndithudi, iye anali. Mukuona kumene iye anachokera? Iye anagwa kuchokera ku Mawu, ndipo anavomereza mbalume. Iye ankayembekezera. . . Mmallo mwa Mzimu Woyera, iye ankafuna munthu woyera, “Dokotala LL., Ph., Q.U.” ndipo kenako anamupanga iye kukhala papa. Mukuona? Ndithudi. Koma, iye, ndicho chimene iye ankafuna, winawake wakuti azimupempherera iye. Winawake. . . Iye ankangolipira ndalama zake, ndipo ndicho chonse chomwe iye ankayenera kuchita. Mukuona?

²⁶⁶ Tsopano, ndicho chinthu chomwecho lero. Basi bola ngati iwo ali nawo mpando woti akhalepo, nkumapereka mochuluka m’mbale ya chopereka, ndizo zabwino mokwanira. Iwo ndi membala wa mpingo umenewo. Musawawuze iwo chirichonse cha Iwo; iwo samafuna kuti adziwe. Ndiwo ana ake aakazi.

²⁶⁷ Tsopano, kodi iye anagwa kuchokera ku chiyani? Kuchokera ku Mawu apachiyambi a atumwi ndi aneneri. Ndiko kumene iye anagwako. Ndiko kumene Achiprotestanti anagwako.

²⁶⁸ Lapani! Bwererani! Tembenukirani mmbuyo nthawi isanathe. Si mochedwa kwambiri panobe. Limodzi la masiku awa Mwanawankhosa uyo adzachoka pa malo Ake, ndipo zikadzatero zidzakhala zitatha pamenepo. Momwemonso ana ake aakazi akupemphedwa tsopano, asanaweruzidwe limodzi ndi iye, kuti “abwerere mmbuyo.”

²⁶⁹ Tsopano, Uthenga wotsiriza umene iwo ati awulandire, ndi pamene mneneri uyu, amene ine ndakhala ndikumukamba. . . Yemwe, ine ndakhala ndikuwerenga mabuku ambiri okhudza Izo. Ndipo ine ndikudziwa kuti anthu enieni abwino, oganiza bwino, oganiza-mwauzimu akudziwa kuti Ichu chikubwera. Iwo akudziwa zimenezo. Iwo akudziwa kuti Ichu chikubwera, mwaona. Iwo. . . Koma vuto lake ndi lakuti, iwo amakhala akunena, “Ife tikuchisowa Ichu. Ichu chidzakhlapo,” ndipo

pamene Icho chidzabwera, kuti icho chidzakhala chodzichepetsa kwambiri, iwo mwinamwake adzachiphonya Icho basi monga momwe iwo anachitira nthawi inayo. Uko nkulondola. Anthu amalemba za Icho, ndi chirichonse, kumati, “Oh, inde, Icho chiyenera kukhala,” ndipo kenako Icho nkudzawonetseredwa pamaso pawo pomwe, ndipo iwo amangopitirira apo pomwe, mwaona. Kotero iwo nthawizonse akhala akuchita zimenezo.

²⁷⁰ Penyani tsopano, Mawu apachiyambi. Iwo ana... iwo... Iye ayenera kulapa, kuti abwerere mmbuyo, komabe, kotero momwemonso ana ake aakazi apemphedwa. Kuti akakamizidwe... iwo adzaweruzidwa, ndi kuponyedwa mu kama yemweyo ndi kudzaphedwa limodzi ndi iye. Iwo apemphedwa kuti abwerere mmbuyo ku Mawu apachiyambi, abwerere ku Chiphunzitso chautumwi. Koma, iwo amangiridwa kwambiri pansi ndi tizikhulupiriro tawo ndi zinthu, iwo sachita zimenezo. Iwo amangochitonza Icho.

²⁷¹ Ndiye kodi iwo akuchita chiyani? Iwo potsiriza akugwirizana mu fano kwa chirombo, mphamvu ina; zindikirani, ndi kuchita, kwa Mkwatibwi wa Mwanawankhosa, monga iye anachitira mu Chivumbulutso 13:14. Ndi chimene iwo akuchita, kumangozunza, basi chinthu chomwecho. Mipingo ikungotonza basi Mkwatibwi woona wa Khristu, monga Roma wakhala akuchitira konse. Chimodzimodzi basi. Inde, bwana. Akuchita kwa—Mkwatibwi weniweni wa Mwanawankhosa chimodzimodzi basi monga iye anachitira mu Chivumbulutso 13:14.

²⁷² Tsopano zindikirani. Ife tikuwona, mwa Mawu a Mulungu a lonjezo, Iye adza—Iye adzawapha ana ake, zipembedzo, ana ake aakazi, ndi imfa yauzimu. Tsopano, ameneyo ndi Chivumbulutso 2:22. Musaiwale zimenezo. Kupha, ndiko kuyika ku imfa. Ndipo *imfa* ndi “Kulekanitsidwa Kwamuyaya ndi Kukhalapo kwa Mulungu.” Muganizire zimenezo, amzanga. Muganizire zimenezo. Musamadalire mu tizikhulupiriro tiritonse topangidwa ndi munthu. Chirichonse chimene chiri chosiyanana ndi Mawu, inu muzikhala kutali ndi icho.

²⁷³ Tsopano penyani, penyani mu Baibulo apa. Ilo linati dzina lake linali Gehena, ndipo... Ine ndikutanthauza:

... dzina lake *linali Imfa, ndipo gehena inamutsatira iye.*

²⁷⁴ Tsopano, gehena nthawizonse imatsatira imfa, mwachibadwa. Pamene munthu wachibadwa amwalira, gehena inamutsatira iye; ndiwo manda, hade, mwaona, ndizo mwachibadwa. Koma mwauzimu, ndi Nyanja ya Moto, mwaona, chabwino, kulowa mu kulekanitsidwa Kwamuyaya, kumene iwo ati adzawotchedwe.

²⁷⁵ Ndipo—ndipo Malaki 4 anati, “Osawasiyira iwo ngakhale chiputu, kapena nthambi, kapena kanthu kalikonse.” Ndiyo

njira yomwe dziko liti lidzakhale nayo yodziyeretsera lokha kachiwiri, kukonzekera Zakachikwi. Mukuona?

²⁷⁶ Kodi inu mwazindikira, wokwerayo ndi “mwamuna”? Ndipo “iyeyo” anali nalo mu “lake” dzanja; “mwamuna,” mneneri wabodza. Koma mkwatibwi wake akutchedwa mpingo, “mkazi,” Yezebeli. Ahabu; Yezebeli. Bwanji, ziri mwangwiro basi monga chirichonse. Mukuona? Mukuona?

²⁷⁷ *Ana aakazi* ndi “mkazi,” nawonso, koma sakulandira konse utsogoleri wa mwamuna mmodzi; Achiprotestanti, kwa uyo, komabe ndi kahule mu kachitidwe, ka chiphunzitso chawo, chipembedzo, machitidwe. Ndizo basi...Ndizo zimene ilo limanena.

²⁷⁸ Zindikirani. Kodi zonsezi zikubwera ku chiyani? Tsopano, ife tangotsala ndi pafupifupi thwelovu, maminiti fortini pano, ine ndikuganiza. Onani kumene zonsezi zikufikako. Ndi chiyani chimenecho? Izo zikubwerera kumbuyo komwe momwe izo zinachitikira, ndi momwe zinayambira Kumwamba. Izo zikufika ku nkondo ya nthawi yotsiriza.

²⁷⁹ Chinthu choyamba, Kumwamba, kunali nkondo. Lusifara anakankhidwira kunja, ndipo anabwera ku dziko lapansi. Kenako iye anawononga Edeni; ndiye iye wakhala akuwononga kuyambira pamenepo. Ndipo tsopano, kuchokera ku nkondo ya Kumwamba, izo zikubwera ku nkondo ya pa dziko lapansi; ndipo iyo ili yoti idzathere, padziko lapansi, pa nthawi yotsiriza, mu nkondo yotchedwa Armagedoni. Tsopano, aliynese akudziwa zimenezo. Nkhondoyo inayambira Kumwamba, yoyera, ndipo kotero iwo anamukankhira iye kunja. Mikaeli ndi Angelo Ake anamugonjetsa iye, anathamangitsidwa. Ndipo pamene iwo anatero, anatsikira komwe ku Edeni, ndipo apa inayambika nkondoyo pansi apa. Met... .

²⁸⁰ Mulungu anali nawo ana Ake akutetezedwa ndi Mawu Ake. Ndipo Eva anatulutsira khosi lake panja, anati, “Ine ndikukhulupirira kuti iwe ukulondola, mwinamwake.” Ndipo pamenepo iyo inayamba. Ndipo yakhala ilipo, kuyambira pamenepo. Kenako Mulungu anabwera pansi, ndipo tsopano Iye ayenera kuti...Iye anabwera pansi kudzawombola iwo amene akanadzabwera pansi.

²⁸¹ Monga ine ndinanenera, Mulungu ali ngati womanga wamkulu. Iye amayika zida Zake zonse padziko lapansi, ndipo akatero Iye amamanga nyumba Zake. Tsopano kumbukirani, pasanakhale njere ya—ya mbewu padziko lapansi, pasanakhale dzuwa lomwe linawalirapo konse pa dziko lapansi, thupi lanu linali likugona pa dziko lapansi, chifukwa inu ndinu fumbi la dziko lapansi. Mukuona? Inu muli. Mulungu ndi Womanga.

²⁸² Tsopano, njira yomwe Iye akanamadzachitira izo, inali kufika pansi ndi kudzatenga (monga Iye anachitira ndi Adamu) mulu waung’ono wa kashiyamu, potashi, ndi kuwala kwa

dziko, ndipo, “Psyii!” Kudzati, “Ndi uyo mwana Wanga wina.” Mukuona? Kenako Iye nkudzabweretsa zina zochulukirapo, ndi, “Psyii!” “Ndi ameneyo winanso.”

²⁸³ Koma kodi Eva anachita chiyani? Iye anawononga njira imeneyo. Ndipo iye anayibweretsa iyo kupyolera mu mchitidwe wa kugonana, kenako imfa inachikantha icho.

²⁸⁴ Tsopano kodi Mulungu akuchita chiyani? Iye ali nazo zochuluka kwambiri za mbewu zimenezo kudutsa kumeneko, zomwe ziri zokonzedweratu; zochuluka kwambiri, zokonzedweratu. Ndiyeno, pa nthawi yotsiriza, Iye sadzanena kuti, “Eva, bwera udzabereke mwana wina.” Iye adzati (“Psyii!”) adzayitana, ndipo ine ndidzayankha. Ndizo zonse. Ndi zimenezotu. Ndiro lingalirolo. Pamene mmodzi wotsirizayo adzalowetsedwa mkati, izo zidzakhazikitsa zimenezo.

²⁸⁵ Tsopano, nkondoyo inayambira Kumwamba. Iyo idzathera pa dziko lapansi, mmawonekedwe a Armagedoni.

²⁸⁶ Tsopano tiyeni tiyang’ane ndipo tiwone izo zikufutukuka. Ndipo mwinamwake ife tikhoza kuchifutukula icho. Ambuye atithandize ife pakali pano kuti tichite ichi tsopano. Penyani icho chikufutukuka.

²⁸⁷ Wokwera wachinsinsiyu, penyani chimene iye akuchita tsopano; “anatsutsa,” anakana kuti alape ndi kubwereranso ku Mawu a Magazi apachiyambi. Mawu anadzakhala Magazi ndi thupi. Mukuona? Iye anakana kuti abwerere kwa Iwo. Ndi wotsutsakhristu! Mkwatibwi woona wa Mawu, ndi wotsu-... iye ndi wotsutsa kwa Mkwatibwi woona wa Mawu. Akutenga mkwatibwi wake yemwe! Iye akumutsutsa Mkwatibwi woona uyu, aponso. Ndipo iye akumutenga mkwatibwi wake yemwe, ndi kumubweretsa iye kwa iye, mmawonekedwe a chipembedzo chotchedwa tizikhulupiriro ndi mbalume. Mukuona? Ndipo tsopano, pomuwona Mkwatibwi woyera uyu, iye akutsutsana naye Iye. Koma iye akumupanga mkwatibwi wakewake, wotchedwa wotsutsakhristu, mwa kuphunzitsa kotsutsakhristu, kumene kuli kosagwirizana ndi Khristu. Mukuona momwe iye aliri wothyathyalika? Ndipo tsopano, mmalo mokhala ndi umodzi wa chikondi, kulamulira, kupembedza pansi pa Magazi, iye ali ndi chipembedzo. Mmalo mokhala ndi Mawu, iye anatenga tizikhulupiriro, mbalume, ndi zina zotero.

²⁸⁸ Monga, ndipo Achiprotestanti amati, “Kachikhulupiriro ka Atumwi.” Ine ndikufuna kuti inu mupeze liwu la iko mu Baibulo. Mtumwi, mulibemo Kachikhulupiriro ka Atumwi mu Baibulo.

²⁸⁹ Monga ine ndinanenera apa, tsopano, osati kale kwambiri, kapena kwinakwake. Ngati atumwi anali nako kachikhulupiriro, ndi Machitidwe 2:38. Ndendende basi zonse zomwe ine ndikudziwa kuti iye anali nazo konse. Ndizo zimene iwo ankaitanira aliyense kuti achite. Pamene iye anawapeza ena a iwo amene ankawoneka ngati anali Akhristu, iye anati,

“Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene inu munakhulupirira?”

Anati, “Ife sitikudziwa ngati kuli . . .”

Anati, “Ndiye inu munabatizidwa chotani?”

²⁹⁰ Tsopano, kukhala wobatizidwa mu Dzina la Yesu, kapena mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, kani, izo, ndi zabwino, koma sindizo zonse za izo apobe. Ayi, bwana. Inu mukhoza kubatizidwa ka fifite, monga choncho, ndipo sizingachite ubwino pang’ono kufikira mtima umenewo utasinthidwa ndi Mzimu Woyera. Izo zonse ziyenera kupita limodzi. Zindikirani, ndi—ndi Khristu!

²⁹¹ Wotsutsakhristu akukana Chiphunzitso cha Mkwatibwi woona, ndipo chotero iye akutenga mkwatibwi wakewake tsopano ndipo akumumanga iye, pansi pa kachikhulupiro kakekake. Akumutenga mkwatibwi wakewake ndi kumupanga iye chipembedzo! Iye akubereka zipembedzo zina, monga zalembedwera m’Malemba Oyera awa; akubereka ana aakazi. Ndipo iye saku . . . Iye akudzakhala ndendende basi monga ngati amayi ake, achibadwa, achidziko, achipembedzo; kumamutsutsa Mkwatibwi wauzimu, Mawu.

²⁹² Iwo samanena kuti iwo si a mpingo. Inu mukayankhula ndi munthu wachipembedzo. “Ndithudi, ine ndi wa mpingo.” Kodi ndinu Mkristu? “Ine ndi wa mpingo!” Izo ziribe chinthu chimodzi chochita nacho Icho! Iwo amati . . . Iwe si wa Mpi- . . . Iwe, iwe ukhoza kukhala wa chimene chimatchedwa mpingo, mwaona, kukhala wa mpingo. Umenewo si Mpingo. Iyo si Mipingo. Amenewo ndi ma loji kumene anthu amasonkhana limodzi, ndipo anthu monga, “mbalame za nthenga zofanana.”

²⁹³ Koma ndinu Mpingo umodzi wokha, ndipo ndiro Thupi lachinsinsi la Khristu. Ndipo inu simumajowina Iwo. Inu mumabadwira mwa Iwo.

²⁹⁴ Monga ine ndakhala ndikunenera nthawizonse, ine ndakhala ndiri ndi banja la a Branham kwa zaka fifite-firii, ndipo sindinajowinepo konse ilo. Ine ndinabadwira mmenemo. Mukuona?

²⁹⁵ Tsopano zindikirani. Izo zikungofanizidwa mokongola. Ine—ine ndiri nalo . . . Lemba ndalemba pansi apa, koma ine . . . ife tiribe nthawi kuti tifike kwa ilo; monga Esau ndi Yakobo.

²⁹⁶ Tsopano, Esau anali munthu wachipembedzo. Iye sankadzinenera kuti anali wosakhulupirira. Iye ankakhulupirira mwa Mulungu yemweyo yemwe Yakobo ankamukhulupirira, Mulungu yemweyo yemwe abambo ake ankamukhulupirira. Koma iye anali chabe shasha, kapena pepani chifukwa cha katchulidweko, basi . . . Iye anali basi wosakhala bwino. Iye—iye anali, tsopano, ponena za kukhala wamakhalidwe, iye anali kwenikweni a—munthu

wamakhalidwe abwino kuposa momwe Yakobo analiri. Koma, inu mukuona, iye sankaganiza . . . “Oh, ufulu woyamba kubadwa uwo uli nacho chochita chanji ndi Ichu?” Ndipo iye anagulitsa ufulu wake woyamba kubadwa kwa Yakobo. Mukuona?

²⁹⁷ Koma, Yakobo, iye analibe zinthu zazikulu, ndipo monga Esau analiri. Iye analibe cholowa chomwe iye anali nacho. Koma panali chinthu chimodzi chimene Yakobo ankachifuna, chinali ufulu woyamba kubadwa uja. Iye analibe nazo kanthu momwe iye akanawupezera iwo; iye anali woti awupeza iwo. Ndipo Mulungu anali nako kulemekeza kwa iye.

²⁹⁸ Ndipo, ndiye, ndicho chinthu chomwecho lero, ndi munthu wachibadwa, malingaliro achithupithupi, wolingalira mwadziko. “Chabwino, ine ndine wa mpingo wa boma. Ine ndine wa mpingo *uwu*. Ine ndine wa *uwu*.” Izo ziribe chinthu chimodzi chochita nacho Ichu, palibe chinthu.

²⁹⁹ Yang’anani, akuwasonkhanitsa iwo tsopano pa kavalo wake wamitundu yosakanikirana. Iye akuwasonkhanitsa iwo pamodzi, pa kavalo wake wa mitundu yosakanikirana, chifukwa iye ali nayo mphamvu ya ndale.

³⁰⁰ Inu simukukhulupirira kuti iye alinayo? Kodi Purezidenti uyu wangolowa chotani posakhalitsapa? Kodi zimenezo zinazemberamo chotani? Uh-huh! Anabwera kuno chifukwa cha ufulu wa chipembedzo; ndipo inu gulu la a democrat amene munagulitsa maufulu anu obadwa nawo ku ndale! Ine ndiribe. . . Chipani cha democrat ndi zabwino; izo zonse ndi zovunda. Ine ndikuyankhula za Chikhristu. Koma inu mukugulitsa maufulu anu obadwa nawo, pa chiphaso cha democrat, kuti muyikemo chinachake monga chimenecho. Manyazi pa inu!

³⁰¹ Kodi inu simukuzindikira kuti fuko lino, mofanana, likufanizidwa ndi Israeli? Kodi Israeli anachita chiyani? Iye anabwera ku dziko lachirendo uko, ndipo anawatengera okhalamowo kunja ndi kuwapha iwo, ndipo analowamo ndi kukatenga dzikolo. Ndicho chimene ife tinawachitira; Amwenye. Ndiwo Achimerika owona okhawo amene alipo, ndi amzathu Achimwenye.

³⁰² Ndiyeno kodi iwo anachita chiyani? Israeli anali nawo amuna ochepa opambana. Chinthu choyamba inu mukudziwa. . . Iwo anali ndi Davide, ndipo iwo anali ndi Solomoni. Iwo anali nawo amuna opambana. Ndipo potsiriza iwo anatenga chigawenga kumtunda uko, Ahabu, yemwe anakwatira Yezebeli, wosakhulupirira.

³⁰³ Chabwino, ndicho chinthu chomwecho chimene ife tinachita. Ife tinali naye Washington ndi Lincoln, koma taonani chimene ife tiri nacho tsopano. Ndipo chinthu chomwecho cha ichu, ndicho, iye wakwatira, ndipo akuledzera ndi kulochedwa-mu-ubweya kwa Yezebeli. Iye akhoza kukhala

munthu wamtundu wabwino, koma mkaziyo aziyendetsa ntchitoyo. Ndipo inu mukuziwona izo pakali pano, banja lonsele likubwera mkati.

³⁰⁴ Mzimu Woyera unandiuza ine chiyani, pafupifupi zaka sarte-faivi zapitazo? Ndipo inu nonse a masiku akale mukuzidziwa zimenezo, za zinthu seveni zimene zikanadzachitika asanafike matsiriziro. Ndipo ichi ndi chotsiriza, chotsatira kwa chinthu chotsiriza, chimene chikubwera. China chirichonsecho chinangogunda ndendende basi pa dontho, ku nkondo ndi china chirichonse. Mukuona? Ndipo tsopano iye ali mmanja momwe, mkazi, kuti alamulire fukoli. Yezebeli! Mukuona?

³⁰⁵ Koma, kumbukirani, mmasiku a Yezebeli, winawake anawawuza kwenikweni iwo mawanga awo. Mukuona?

³⁰⁶ Kusonkhanako, pa kavalo wawo wamitundu yosakanikirana. Ndipo, mwaona, iye akusonkhanitsa chinthu ichi pamodzi, chosakanikirana ndi tizikhulupiriro, chipembedzo, ziphunzitsa zopangidwa ndi anthu. Nkulondola uko? Ndithudi, mtundu wosakanizika, mtundu wosakanizika wa kavalo wakufa, wotumbululuka wa mdziko! Tsopano, uko nkulondola. Mitundu yosakanizika ya kavalo wakufa, mawonekedwe achidziko a kavalo wotumbululuka, oh, mai, wopanda Magazi oyera a Mawu, nkomwe!

³⁰⁷ Ndipo penyani. Kuchokera ku ngodya... “Kuchokera ku ngodya zinayi za dziko lapansi, iwo akuwasonkhanitsa iwo; akuwasonkhanitsira iwo ku Armagedoni,” Baibulo linatero. Ine ndikuyesetsa kuganiza za Malemba, monga ine ndawalembera iwo pansi apa. Ine sindikuwatchula iwo; koma basi pamene iwo alembedwapo, kuwona chimene iwo ali. “Akuwasonkhanitsira iwo pamodzi, ku tsiku lalikulu la nkondo ya Ambuye Mulungu.” Penyani. Tsopano, pa kavalo wamitundu-yosakanikirana uyu, wachidziko, wotumbululuka, wodwala, tangoganizani za zimenezo; inu mukudziwa, ndicho chinthu choipa. Tsopano penyani kumene iye akuwasonkhanitsira iwo, “Kuchokera ku ngodya zinayi za dziko lapansi.” Iwo akusonkhanira tsopano ku chiwonetsero. Chiwonetserocho chidzakhala pa “Armagedoni,” malingana ndi Mawu. Mukuona?

³⁰⁸ Pa kavalo wotumbululuka, atakwera pa iye, ali ndi “Imfa” itamatidwa, kapena, ali ndi dzina litamatidwa pa iye, “Imfa,” wotsutsakhristu! Mvetserani. Wotsutsakhristu, chipembedzo choyamba (icho sichingatsutsidwe); ali ndi Yezebeli wake, hule kwa Mawu; ali ndi ana ake aakazi, limodzi ndi iye, Achiprotetanti; akudzisonkhanitsa okha pamodzi tsopano mu umodzi!

³⁰⁹ Kodi inu munawamva anthu Achibaptisti akuyankhula tsiku lina cha kuno, inu mukudziwa? Huh? “Oh, ife sitiwajowina iwo, koma ife tizi—ife tiziyanjana nawo ndi kumakhala ngati

tikukondana nawo iwo. Ife sitisowa kujowina mpingo wawo, koma. . .” Ndi inu pamenepo. Ndi inu pamenepo, ndendende basi chimene Mawu ananena. Mukuona? Mukuona? Hule wakale, mmalo oyambirira, mwaona.

³¹⁰ Tsopano apa iwo ali, akudzilumikiza okha pamodzi, akubwera ku chiwonetsero chimenecho, ku Armagedoni, ndipo akukwera pa kavalo wamitundu yosakanikirana; ndi kavalo mmodzi woyera, kavalo mmodzi wofiira, kavalo mmodzi wakuda. Atatuwo, osiyanasiyana: yandale—mphamvu yandale, mphamvu yauzimu, zolamuliridwa ndi mphamvu ya ziwanda, imene ili yotsutsakhristu. Mukasakaniza zonsezo pamodzi, ndipo inu mukhala ndi chotumbululuka, chinthu chowoneka-modwala chimene iye wakwerapo. Kulondola. Tsopano zindikirani. Taonani chimene iye akukwerapo, kavalo uyu wamawonekedwe-otumbululuka, kavalo wamtundu-wotuwa, wosakanizika ndi kuda, kufiira, ndi kuyera; akubwera ku nkondo, akusonkhanitsa omumvera ake kuchokera ku fuko lililonse pansi pa Kumwamba! Kodi Daniele sanatanthauzire lotolo, ndi ufuna mzere uwo wa chitsulo ukuyenderera kulowa mu ufumu uliwonse, wa Roma? Apa iwo akubwera, akusonkhana.

Tsopano khalani chete potseka, miniti yokha, ndipo mvetserani mwatcheru.

³¹¹ Iwo akusonkhana mmenemo tsopano kudzachita zimenezo, kubweretsa omumvera ake kuchokera ku ngodya zinayi za dziko lapansi; akukwera kavalo wotumbululuka, wodwala, wamitundu itatu, wosakanizika. Munthu yemwe yemweyo!

³¹² Tsopano, mu Chivumbulutso 19, si yekhayo amene akukonzekera, koma Khristu akukonzekera kudzakomana naye iye. Nkhondoyo idzakhala yotentha ndi yamphamvu. Khristu, mu Chivumbulutso 19. Khristu akuwasonkhanitsa Ake, osati kuchokera ku ngodya zinayi za dziko lapansi, chifukwa padzakhala otsalira apang’ono chabe. Kodi Iye akuchita chiyani? Iye akuwasonkhanitsa iwo kuchokera ku ngodya zinayi za Kumwamba. Ife tidzaitenga iyo, “miyoyo ya pansi pa guwa,” mawa usiku, ndipo inu mudzawona ngati izo ziri zowona, kapena ayi. Ngodya zinayi za Kumwamba; pa kavalo woyera mwa chipale!

³¹³ Iye alinso ndi Dzina, osati imfa, koma, “Mawu a Mulungu,” Moyo. Amen. Analilemba pa ntchafu Yake pomwe apa, “Mawu a Mulungu.” Ndiwo Moyo wokhawo, chifukwa Mulungu ndi yekhayo gwero la Moyo Wamuyaya umene ulipo. Zoe! Nkulondola uko?

³¹⁴ Ndipo Iye ali nalo litalembedwa, “Moyo,” akukwera pa kavalo woyera; ndipo apa pali mwamuna yemwe ali nazo mphamvu zitatu zosiyanasiyana zosakanizika, wotchedwa “Imfa.” Akusonkhanitsa nthumwi zake zapadziko lapansi;

ndipo Khristu akusonkhanitsa omumvera Ake obadwira Kumwamba, oyera. Iye ali ndi “Imfa” italembedwa pa iye; Khristu ali ndi “Moyo” utalembedwa pa Iye.

³¹⁵ Iwo amene ali ndi Iye ali pa akavalo woyera, nawonso, ndipo iwo akutchedwa, “Osankhidwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.” Amen! Ndipo iwo ndi okhulupirika ku Mawu. Amen! Psyii! Ine ndikuchikonda chimenecho. “Oyitanidwa, osankhidwa, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.” Ndipo kenako, okhulupirika ku Mawu, mwa kusankha kwawo, onse okondowezeka ndi vinyo watsopano ndi Mafuta, akungokwera motsatira kumene, akubwera pansu kudzakumana naye iye. Iwo akudziwa kuti Mabinguwo adzatiyambitsira ife chinthucho, posachedwa pompa. Mukuona?

³¹⁶ Penyani. Iye akuchita izo motani? Kotero, ngati Iye ali Mawu, ndipo Dzina Lake ndi Mawu, ndiye Mawu ndiwo Moyo. Wotsutsakhristu; chirichonse chomwe chiri *anti* ndicho “chotsutsa,” kotero *anti* ndi “kutsutsa” Khristu, Mawu. Chotero, kayenera kukhala kachikhulupiro, kapena chipembedzo, chimene chiri chotsutsa Mawu.

³¹⁷ Bwanji, ine sindikuwona momwe inu muti muziphonyere zimenezo. Ngati inu—inukuzimvetsa izo, inu mungaziphonye bwanji zimenezo? Ine sindikudziwa momwe inu muti muchitire.

³¹⁸ Ndipo izo ndi zoona. *Anti* ndiko “kutsutsa.” Kodi si kulondola kumeneko? “Kuchotsako kumeneko.” Ndicho chimene iye anali. Iye akukwera kavalo wake wosakanikirana. Iye tinaziwona izo pomwe apa mu Mawu a Mulungu.

³¹⁹ Iye tinaziwona zimenezo uko komwe mu mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Apa Iye akuzibweretsanso izo kumene mu Zisindikizo, akuzitsegula ndi kuwonetsa zinthu izo zimene zinali kupitirira, pansu pa mibadwo ya mpingo.

³²⁰ *Anti* ndi “kutsutsa” Mawu. Mwaona chifukwa chimene, tizikhulupiro, chifukwa chimene ife tiri otsutsa kwambiri tizikhulupiro ndi zipembedzo? Chifukwa izo ndi zotsutsa Mawu. Mukuona?

³²¹ Apa ife tikuwona Moyo ndi imfa zikubwera ku kulimbana kotsiriza. Kavalo woyera, wa Moyo woona; kavalo wotumbululuka, wa kachikhulupiro kosakanikirana. Iwo akuchiwona chinthucho chikubwera ku—ku chiwonetsero chenicheni.

³²² Tsopano ine ndikufuna kunena chinachake apa. Inu mukhoza kusachikhulupirira ichi. Koma ine ndinachifufuza icho, kuti ndikhale wotsimikizika. Pali mtundu umodzi wokha wapachiyambi, ndipo ndiwo woyera. Ndi angati amadziwa zimenezo? Pali mtundu umodzi wokha wapachiyambi. Wina uliwonsewo, umakhala wosakanizidwa.

³²³ Khristu ali pa Mawu olimba-oyera, osakhudzidwa, kuchokera pachiyambi. Ameni! Ameni! Mtundu uliwonse ukanakhala woyera ngati mankhwala ena akanapanda kuthiridwa mwa iwo. Ameni! Ulemelero! Mpingo uliwonse ukanamayima pa Chiphunzitso cha atumwi cha Mawu a Mulungu, ndipo Mulungu nkumawutsimikizira Iwo, ngati iye akanapanda kukhala nato tizikhulupiriro kapena zipembedzo zitasakanizidwa mwa Iwo. Ndi zimenezotu.

Oh, M'bale Evans, ine ndikumverera bwino pakali pano! Inde, bwana. Inde, bwana.

³²⁴ Mtundu umodzi wokha wapachiyambi, ndiwo woyera. Iwo siuli—iwo sunasakanizikane konse ndi zipembedzo kapena tizikhulupiriro. Ayi, bwana.

³²⁵ Ndipo, kumbukirani, oyera Ake avekedwa ndi mikanjo yoyera, osati yosakanizikana ndi zipembedzo ndi tizikhulupiriro. Tsopano ife tikupeza kuti, tizikhulupiriro ta chipembedzo, apa ndi pamene inu mukutengera mtundu wanu wosakanikirana. Koma uwu ndi mtundu wapachiyambi umene Iye akukwerapo. Mtundu wapachiyambi uli pa anthu Ake. Ndipo iwo aviyikidwa m'Magazi, amene anatsuka chovala chimenecho, ndi kuchitumiza icho kumbuyo komwe uko. Mukuona? Uko nkulondola.

Iwo amene anasakaniza, anasanduka otumbululuka ndipo akupita ku imfa.

³²⁶ Iko ndi kupotoza, kupotoza, kusakaniza mitundu ndi woyera; iwe umapotoza mtundu wapachiyambiwo. Nkulondola uko? Ngati mtundu wapachiyambi, mtundu wokhawo, ulipo ndi woyera, ndipo iwe ukasakaniza chinachake kwa iwo, iwe upotoza cholinga chake chenicheni. Ameni. Nkulondola uko?

³²⁷ Ndipo, pamene, ngati Iye ali kavalo woyera, ndipo Iye ndi Mawu; ndiye, kuti usakanize chirichonse ndi Iwo, mtundu uliwonse wa kachikhulupiriro, kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo, kuchotsa Mawu amodzi kwa Iwo, ndiko kupotoza chinthu chonsecho. Oh, mai! Ndisungeni ine limodzi ndi Mawu, Ambuye!

³²⁸ Choonadi ndi cholakwika! Oh, mai! Ziribe kanthu kaya nzabwino bwanji kuti ndi... Choonadi ndi cholakwika sizingasakanikirane. Izo sizingasakanikirane. Izo mwinamwake ndi PAKUTI ATERO AMBUYE kapena ndi zolakwika. Ziribe kanthu kaya bambo woyera ananena chiyani zimenezo, Bonifer Woyera, kapena—kapena bishopu wamkulu wa Canterbury; ine sindikumudziwa amene ananena zimenezo. Ngati izo ziri zotsutsana ndi Mawu, ndi chisokonezo. Izo sizingasakanikirane. Mukuti, “Bwanji, munthu uyu anachita...” Ine sindikusamala chimene iye anachita, kaya iye ndi woyera chotani, kapena chirichonse chonga icho. *Ich*i ndi Choonadi cholunjika chokhacho chimene ife tiri nacho. Palibe mpingo, palibe

kachikhulupiriro, ziri ndi Choonadi, ngati izo ziri kunja kwa *Ich*.

329 Ndipo ndiwonetseni ine mmodzi amene ali nacho Icho. Basi, ine ndikufuna kuti inu mundiuze ine. Ine nditsecula tsamba mu Baibulo, ndipo ndikuwonetsani inu chinachake. Mukuona? Tchulani mmodzi yekha. Inu mukuti, “Wachipentekoste.” Oh, mai! Ine ndinangogwira lingaliro limenelo kuchokera kwa winawake apo. Ndicho chifukwa chake ine ndinanena zimenezo. Kulibwino ndingochisiya icho chokha, pakali pano, chifukwa ine ndinawona kuti icho chinayambitsa malo a chironda apo pomwe. Ine sindinati—sindinafune kukupwetekani inu, koma ine—ine ndimangofuna kuti inu mudziwe kuti ine ndimadziwa chimene inu mumaganiza. Mukuona?

330 Iwo amene anasakaniza, anadzakhala (anti) imfa. Iwo amasandulika mtundu wa imfa, pamene iwe usakaniza mtundu uliwonse wa chirichonse ndi chapachiyambi.

331 Izo ziri monga Khristu ananenera zokhudza mbewu ya mpiru. Komabe, ndiyo yochepetsetsa ya mbewu zonse, koma siyimasakanikirana ndi chirichonse. Mpiru sumasakanizidwa. Iye ndi mpiru weniweni. Kotero ngati inu muli nacho chikhulupiriro chochuluka chomwecho, ingogwiritsitsani kwa icho.

332 Zindikirani. Moyo unatsatira, wokwera pa kavalo woyera, Yemwe anali Mawu, Moyo, wotsimikiziridwa ndi oyera Ake owukitsidwa amene anali Iye. Tsopano kodi nkhoodoyi idzayenda motani?

333 Yesu anati, “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye atafa, komabe iye adzakhala moyo.” Iye anati, “Ngati inu mukhulupirira mwa Ine, ngakhale inu—inu mutafa, komabe inu mudzakhala moyo. Ndipo yense amene akhala moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse.” Ndiponso, Iye anati, “Iye amene akhulupirira mwa Ine. . . Iye adzamupatsa iye Moyo Wamuyaya, adzamuukitsa iye pa tsiku lotsiriza.” Ndiro Lemba Lake lolonjezedwa.

334 Apa pakubwera Satana, limodzi ndi ngodya zinayi zonse za dziko lapansi, limodzi ndi Achiprotestanti ake ndi ake—Akatolika ake, ndi onse limodzi, akuguba chamtsogolo kupita ku Nkhondo ya Armagedoni. Chabwino.

335 Ndipo apa pakubwera Yesu, akubwera pansi kuchokera Kumwamba, limodzi ndi oyera owukitsidwa, Mawu otsimikiziridwa.

336 Ine ndinati, ngati Mulungu ayankhula, kapena akakutuma iwe, Iye ali. . . Iye—Iye amayikira kumbuyo chimene iwe ukuyankhulacho. Mukuona? Zindikirani, ngati ndiwe kazembe wochokera Kumwamba, Kumwamba konse kumakhala kumbuyo kwako. Ndipo Kumwamba ndi kopangidwa ndi Mawu. Uh-huh.

³³⁷ Zindikirani, tsopano, Iye wabwera ndi oyera owukitsidwa, kutsimikizira kuti Mawu Ake ndi owona.

³³⁸ Kotero Satana akudziwa, ndiye, kuti maphompho opanda malire amukonzekera iye. Mukuona? Oh, mai! Pamene, imfa inkakwera kavalo-wotumbululuka, wosakanizidwa ndi tizikhulupiriro ndi zipembedzo, ndi kumamutsatira iye, oh, mai, ku kulekanitsidwa Kwamuyaya ndi Mulungu. Ndiko kumene iye anawayendetsa iwo, ku kulekanitsidwa Kwamuyaya.

Khristu anawuyendetsa Mpingo Wake mpaka kukalowa mu Ulemelero, mu chiwukitsiro.

³³⁹ Zindikirani ndime ya 8 tsopano, basi mpaka...gawo lotsiriza la ndime ya 8, pamene ife tikutseka, mwaona.

...mphamvu inapatsidwa kwa iwo...

³⁴⁰ Ndi ndani “iwo”? Mukuona? Chabwino. Wotsutsakhristu, wotchedwa “Imfa.” “Gehena inatsatira.” Taonani kachitidwe kake ka nsonga-zinayi.

³⁴¹ Wotsutsakhristu, kavalo woyera; akupha mwa mzimu, pokhala wotsutsakhristu; kupha mwauzimu.

³⁴² Nambala thuu, kavalo wofiira; amapha ndi lupanga; mphamvu ya ndale, pamene mpingo ndi dziko zinalumikizana.

³⁴³ Kavalo wakuda; miyoyo, pamene iye anapereka chiphunzitso chake, ndipo iye anachita kumeneko ndi ziwerewere zake. Ndipo iye ankayeza chakudya chawo, ndi a...kugulitsa chawo... zimene iwo ankapereka kukhala chakudya, kwa muyezo, ndi ndalama, ndi zina zotero.

³⁴⁴ Wachinayi, kavalo wotumbululuka; Kulekanitsidwa Mwamuyaya ndi Mulungu. Anayi, kachiwiri, mwaona. Oh, mai!

Matamando akhale kwa Mulungu!

³⁴⁵ Tsopano, potsiriza, apa potseka. Kwa iwo...Kodi inu muli nayo...Ine ndapitiriza nthawi, koma kodi inu mungandipatse ine pafupifupi maminiti ena teni? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ine ndiri nako kuyitana kochuluka, lero, kokhudza—kokhudza kuyankhula kwanga pano.

³⁴⁶ Panakhala zotentheka zambiri zomwe zinayambika, zokhudza Eliya, mpaka izo zinangokhala...Izo—izo zinakhomereredwa ku kufa. Ndipo inu mukhoza... Chabwino, mungolola...Mulungu angondithandiza ine kuti ndikuthandizeni inu kuti muwone chimene ine ndikuyang'anapo. Kodi inu mutero? Tiyezi tingoyesera kutero, mwaona.

³⁴⁷ Tsopano apa pali, potseka, kwa iwo amene sakukhulupirira kuti mtumiki wotsiriza ku m'badwo wa mpingo ndi Eliya mneneri, mwamuna wodzozedwa mwa mzere umenewo.

³⁴⁸ Ikadzachitika imfa...Yang'anani. Ikadzachitika imfa, ya m'badwo wa mpingo wotsiriza uno...Tsopano, inu mukuzindikira chimene chinachitika, mukuona. Ikadzachitika imfa, matupi awo akufa adzawonongedwa ndi zirombo zakuthengo. Inu mukudziwa zimenezo. Tsopano, izo nzoona. Monga awo, anali ndi choyimira cha Yezebeli.

³⁴⁹ Tsopano tsegulani ku Chivumbulutso 2:18 ndi 20. Ine ndikukhulupirira tinapapeza pamenepo maminiti pang'ono chabe apitawo. Sichoncho ife? Eya, ine ndikukhulupirira ife tangopapeza kumene pamenepo. Ine ndinali nazo izo zitalembedwa apa kwa ena...Inde. Nthawi ya kuvunda kwa makhalidwe, ndicho chimene icho chinali. Mwaona momwe izo zinachitikira, momwe Yezebeli anabwereramo. Tsopano, Yezebeli ndi mipingo, mpingo wamakono uwu; osati Mkwatibwi, tsopano. Yezebeli, mu Chipangano Chakale, ali choyimira cha mpingo lero, molingana ndi Mawu a Mulungu, a Chivumbulutso 2:18, 20.

...iwe ukumulola mkazi uja Yezebeli, yemwe anadzitcha yekha mneneri wamkazi,...

³⁵⁰ Mukuona? Nkulondola uko? Tsopano, izo zikufanizidwa mwangwiro ndi Yezebeli. Tsopano, choyamba...

³⁵¹ Ife tikanakhoza kumangokupatsani inu Lemba pambuyo pa Lemba, mwaona, kuti m'badwo wotsiriza ndiwo Uthenga wa uneneri kwa Mpingo, kuwaitanira iwo kuti abwerere ku Mawu apachiyambi. Tsopano zindikirani. Nkulondola uko? Malaki 4 ananena chomwecho, ndi enawo, Chivumbulutso 10:7, ndi kumapitirira mpaka mmusi. Mukuona? Yesu Mwiniwake ananeneratu zimenezo, mmusi, mmusi, mmusi. “Monga izo zinali mmasiku a Loti,” ndi zina zotero monga choncho, ndipo mpaka mmusi. Izo zikumangobwerabe mpaka mmusi.

³⁵² Yezebeli ali choyimira cha mpingo wamakono lero chifukwa Akatolika ndi Achiprotestanti alumikizana pamodzi tsopano. Apo—apo palibenso kuchilambalala chimenecho. Iwo onse ndi zipembedzo, kotero ndizo basi—basi ziri ngati mayi ndi mlongo wake, ndizo zonse. Iwo amakangana ndi kutsutsana wina ndi mzake, koma iwo ali chinthu chomwe chomwecho, onsewo ndi timahule. Tsopano, ine sindikunena zimenezo mwa ine ndekha. Ine ndikuzitenga kuchokera ku PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona? Chabwino.

³⁵³ Tsopano ife tikuzindikira, anaphedwa mwa kulamulira kwa Mulungu, anali Yezebeli, anaphedwa chifukwa Mulungu anamutuma Yehu kuti apite kumusi uko ndi kukamuponyera iye kunja pa zenere, ndi kumupha Yezebeli. Ndipo agalu anadya thupi lake (nkulondola uko?), Yezebeli weniweniyo. Ahabu, mfumu yake, mutu; agalu ananyambita magazi ake, monga momwe Eliya woyambayo ananeneratu. Mwaona komwe ife tikupita, sichoncho inu?

354 Chifukwa chiyani? Eliya woyambayo anali mwamuna wokanidwa, ndi mipingo. Ndipo Yezebeli ndi Ahabu anali mitu ya mipingo imeneyo, mpingo ndi boma, zonse palimodzi. Ndipo Elisha anawulula machimo a Ahabu kwa iye, ndipo analamulira mpingo wonse kuti ubwerere ku Mawu owona.

355 Ngati icho sichiri ndendende chimene Eliya wachiwiri akuyenera kudzachita pamene iye adzabwere ku mpingo uwu mu tsiku lino, “kudzabwezeretsanso Chikhulupiriro chapachiyambi”! Ine sindikudziwa momwe inu muti muthawire kwa Ichu. Uko nkulondola. Kubwerera ku Mawu owona! Uko nkulondola.

356 Tsopano ngati mukufuna kuwawona matupi awo, tiyeni titsegule apa ku Chivumbulutso 19, atatha—atatha Mawu kuwadula iwo. Tsopano, Mawu adzawapha iwo. Inu mukudziwa zimenezo. Chabwino. Tsopano inu mungoyang’ana ndi kuwona chimene chidzachitike pamene Khristu Akubwera, mu Chivumbulutso 19, kuyambira ndi ndime ya 17.

Ndipo ndinawona mngelo atayima mu dzuwa; . . .

357 Tsopano, apo nkuti zitangochitika kumene, yang’anani pamwamba apa, “Ndipo chovala Chake chinali chitaviikidwa mmagazi. Ndipo Iye akutchedwa MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE.” Mu ndime ya 13, “Iye akutchedwa Mawu a Mulungu.” Mukuona? Tsopano, apa Iye ali, “MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE.”

Ndipo ine ndinawona mngelo . . .

358 Tsopano penyani. Iye akupitirira.

Ndipo kuchokera mkamwa mwake mukutuluka lupanga lakuthwa, kuti ndi ilo iye akakanthe nalo mafuko: . . .

359 “Kuchokera mkamwa Mwake,” monga kuchokera mkamwa mwa Mulungu kupita mkamwa mwa Mose. Mukuona?

. . . ndipo iye adzawalamulira iwo ndi ndodo yachitsulo: ndi . . . kuponda moponderamo mpesa—moponderamo mwa ukali ndi mkwiyo wa Mulungu Wamphamvuzonse.

Ndipo iye ali nalo pa chovala chake dzina . . . pa ntchafu yake dzina lolembedwa, MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE.

Ndipo ine ndinawona mngelo . . .

360 Tsopano penyani. Tsopano Iye akutulukira, akukantha. Iye akumukantha ndani? Yezebeli ndi Ahabu wake, mneneri wabodza.

Ndipo ine ndinawona mngelo atayima mu dzuwa; ndipo anafuula ndi liwu lokweza, kunena kwa mbalame zonse za mmlengalenga mkati mwa miyamba, Mubwere

ndipo mudzadzisonkhanitse nokha pamodzi ku phwando la Mulungu wamkulu;

³⁶¹ Iye akuwadyetsa iwo kwa zinyama ndi mbalame. Tsopano penyani cha apa mu mutu winawu apa, wa Bukhu la Chivumbulutso. Ndipo, miniti yokha, “Kupha ndi lupanga, ndi imfa, ndi zinyama za padziko lapansi.” Mukuona? Mpingo wa Yezebeli, thupi lake (lenileni), liri lakuti lidzadyedwe ndi mbalame ndi zinyama za padziko lapansi. Chimodzimodzi basi monga Ahabu ndi Yezebeli anachitira, mwa chibadwa, momwemonso iwo adzachita, mwa mawonekedwe auzimu, mpingo. Kodi inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino.

³⁶² Wa Eliya... Oh! Eliya anali mneneri mmasiku a Ahabu ndi Yezebeli, mwachibadwa. Ndipo iye walonjezedwa kuti adzachita chinthu chomwecho, molingana ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, mu Mawu, kwa Yezebeli, mwauzimu; utumiki wake wamawonekedwe a Mzimu.

³⁶³ Penyani. Eliya, ngakhale, mu tsiku lake, anatsimikiziridwa mwabwinobwino ndi mwakuya, sanakhoze kuwatembenezira iwo kubwerera ku Mawu. Nkulondola uko? Ngakhale, Eliya anayesetsa, ndi chirichonse. Iye anachita chirichonse. Iye— iye anawawonetsa iwo zizindikiro ndi zodabwitsa; ndipo iwo anaseka munkhope yake. Chinthu chomwecho iwo adzachita ndi wauzimu apa, mwaona. Iye sanakhoze kuwatembenuza iwo kubwerera ku Mawu. Kuchokera mu mamillioni...

³⁶⁴ Tsopano mvetserani, mpingo, mwatcheru tsopano, inu amene mwasokonezeka pang’ono pa izi.

³⁶⁵ Kuchokera mmamillioni m’dzikolo, mmasiku a Eliya, pamene Yezebeli ndi Ahabu ankalamulira, mwa—mwa choyimira cha chenicheni lero; kuchokera mu dziko lonse, uko kunali seveni handiredi okha opulumutsidwa, mwa kulalikira kwa Eliya. Nkulondola uko? Ndizo ndendende.

³⁶⁶ Penyani, Eliya sankadziwa konse ngakhale mmodzi wa iwo kuti anali mwanjira imeneyo. Iye ankaganiza kuti anali mmodzi yekhayo wopulumutsidwa, mpaka Mulungu anatsegula chimodzi mwa Zisindikizo ndipo anamuwonetsa iye chinsinsi mu Bukhu, kuti Iye anali nawo seveni handiredi amene sanagwadire konse ku tizikhulupiro timeneto tomwe iwo anali nato. Pamene Mulungu anatsegula Bukhu Lake kwa Eliya, anati, “Tsopano dikira miniti, mwana. Ine ndiri nawo seveni handiredi amene ayikidwa kumeneko, kunja uko, amene ali nawo maina awo pa Bukhu chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi. Iwo ndi Anga.” Psyii! Mulungu anatsegula Zisindikizo.

³⁶⁷ Ndi chifukwa chake ine ndikuganiza kuti Yohane anali kufuula mochuluka usiku wina. Iye ayenera kuti aliwona dzina lake liri Pamenepo, inu mwaona. Mukuona?

Tsiku lina Mulungu anatsegula...

³⁶⁸ Elisha, iye anali atalalikira. Iye anali atachita chirichonse, ndipo—ndipo—ndipo anawulalikira mtima wake kunja. Iye anachita chirichonse chimene akanatha kutero, ndipo komabe iwo anangokhala odzikuza, ndipo anamutcha iye chirichonse, ndipo anati, “Iwe ndi amene wayambitsa zonsezi. Iwe ndiwe wamizimu. Ndiwe amene ukupangitsa kuti mavuto onsewa abwere. Iwe ndiwe wolakwa,” ndi chirichonse monga icho. Iye ananena chirichonse kwa iye. Yezebeli anawopsyeza kuti awudula mutu wake, ndi china chirichonse. Uko nkulondola. Aliyense anali kumutsutsa iye.

³⁶⁹ Ndipo kenako iye anati, “Ambuye, ine nditatha kuchita zimenezo, zonse zimene Inu munandiuza ine kuti ndichite! Ine ndakhala ndendende ndi Mawu Anu. Pamene Inu munandiuza ine chirichonse, ine ndinali wopanda mantha. Ine ndinayenda mpaka pa nkhope pomwe pa mfumu, ndi china chirichonse, ndipo ndinawauza iwo, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE.’ Ndipo Inu simunandiuzepe ine chinthu, ndipo ine sindinawauzepe iwo chinthu chimodzi, koma chimene chinadzachitika. Ndipo tsopano apa ine ndiri, mmodzi yekhayo amene watsala, kuchokera mu gulu lonselo. Ndine mmodzi yekhayo amene watsala, ndipo iwo akuyesetsa kuti andiphe ine.”

³⁷⁰ Mulungu anati, “Ine nditsegula chimodzi mwa Zisindikizo ndipo ndikuwonetsa iwe chinachake.” Iye anati, “Iwe ukudziwa, Ine ndiri nawo seveni handiredi kumbuyo uko, amene sanagwadirepo konse bondo kwa... sanajowine kalikonse ka tizikhulupiriro timeneto panobe, zipembedzo. Alipo seveni handiredi a iwo okonzekera Mkwatulo, mwaona.” Oh! Oh! Iye ananena kwa mneneri Wake, kwa yemwe Iye amawululirako Mawu Ake, mwaona, kupyolera mu Lembu. “Ine ndiri nawo maina okonzeka seveni handiredi panobe, kuchokera mu m’badwo uno; seveni handiredi a iwo. Iwo sanagwadire maondo awo kwa aliyense” (ngati ine ndinganene izi mu tsiku lino) “zipembedzo za mabungwe, ndi kubwera mwa tizikhulupiriro, mkati mwawo.”

³⁷¹ Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndiye, mophweka icho chiyenera kukhala. Icho basi chiyenera kukhala. Ndipo chiri molingana ndi Mawu. Pamene munthuyo adzafika powonekera, iye adzakhala mneneri. Motsimikiza basi monga mmene ine ndikuyimira pa guwa ili. Mukuona? Ndipo iye adzakhala nawo kumene Mawu amenewo. Iye sadzatengera chikhulupiriro cha aliyense kapena china chirichonse. Uko nkulondola. Iye adzakhala munthu wokonda kuthengo, monga momwe Elisha ankachitira, iye... ndi monga Yohane anabwerera. Iye adza—iye adzadana ndi akazi, (mnyamata!) akazi amakhalidwe oyipa! Psyii! Mnyamata, iye adzawanda pa iwo! Eliya anatero, momwemonso anatero Yohane. Mukuona? Mukuona? Ndipo iye adzakhala mowongoka chomwecho ndi Mawu amenewo. Iye adzakhala—adzakhala wotsutsa

mabungwe. Bungwe? “Musaganize zonena mwa inueni, ‘Ife tiri naye Abrahamu munga atate athu,’ pakuti ine ndikuti Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.” Mukuona? Ndithudi anatero.

³⁷² Tsopano, ndi zimenezotu, amzanga. Apa pali Chisindikizo Chachinayi, chatsegulidwa. Ndipo okwera a akavalo anayi awululidwa, mwa kupambana kwa kudziwa kwanga. Tsopano, izi ndi zonse zimene zinachitika pa dziko lapansi.

³⁷³ Chisindikizo Chotsatira, ife tiwona, chiri Kumwamba, kumene miyoyo ili pansi pa guwa.

³⁷⁴ Tsopano, basi potseka, ine ndikufuna kuyankhula zochepe izi...mawu pang’ono chabe, pomwe apa, amene ine ndawalemba. Ife talumphapafupifupi, pa Zisindikizo zinayi izi, Zisindikizo zinayi zoyamba.

³⁷⁵ Tsopano, mawa usiku, ife—ife tidzasintha malo, kuchokera pa zinthu zapadziko lapansi tidzapita mmwamba. Iye akuyang’ama mmwamba apa ndipo akuwona miyoyo ya pansi pa guwa, guwa, loperekera nsembe.

Usiku wotsatirawo, chiweruzo chikukantha.

³⁷⁶ Ndipo usiku wachinayi, kapena usiku wotsirizawo, Lamlungu usiku, ine sindikudziwa chiyani. Ine sindikudziwa chomwe zina izi zikutanthauza. Ine ndinangoziwerenga izo, munga inu munachitira. Koma, “Uko kunali chete kwa theka la ora,” koma pali chinachake chimene chinachitika. Ine ndikumuyembekezera Iye kuti adzawulule Ichu. Iye adzachita zimenezo. Ndine wokhutitsidwa kuti Iye adzatero.

³⁷⁷ Ife tinachita kupita, ku malo osiyanasiyana a Lemba, ku Chivumbulutso 19, kuti tiwonetsere kuti Kubwera kwa Khristu kudzakupha wotsutsakhristu. Ndi chifukwa chake ine ndinayenera kuzisiya izi, kungotenga ndime ziwirizo. Ine ndimayenera kupita ku zigawo zosiyanasiyana za Malemba, kuti ndikatsimikizire zinthu izi. Kotero ndicho chifukwa chake ine ndinapita ku Chivumbulutso 19, kuti ndikawonetsere kuti mathero a wotsutsakhristu, adzakhala kupha; kwa Khristu, pamene Iye akubwera, Iye adzakupha wotsutsakhristu.

³⁷⁸ Ku Chivumbulutso 10, kuti ndiwonetsere kuti Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri udzakhala munthu, mmasiku ano otsiriza, wodzozedwa ndi Mulungu kwa utumiki chimodzimodzi munga momwe Eliya mneneri anali, munga zinanenedweratu mu Malaki 4, kuti adzawulule Mawu owona a (pachiyambi) Mulungu mu m’badwo uno, Mawu apachiyambi a Mulungu mu m’badwo uno. Monga iye anachitira kwa Yezebeli wachibadwa, chomwechonso munthu uyu adzachita icho kwa Yezebeli wauzimu, mipingo ya chipembedzo. Ine ndinachita kupita ku mutu wa 7...mutu wa 10, ndime za 1 mpaka 7, kuti ndikatsimikizire kuti izo zinali zolondola. Ndi uko ku Malaki, ndi Amosi, ndi ena otero, kuti ndikatsimikizire zimenezo.

379 Eliya anali mneneri amene analosera ndi kudzudzula Yezebeli, mu m'badwo umenewo.

380 Ndipo Eliya sanafe konse. Iye ndithudi sanatero. Iye anadzawonekeranso kachiwiri, zaka zina eyiti handiredi mtsogolo mwake, ali pa mbali pa Yesu Khristu, pa Phiri la Chiwalitsiro. Iye sanafe.

381 Tsopano, ife tikupeza kuti Mzimu wake uli woti udzamudzoze munthu, molingana ndi lonjezo la Mulungu, mmasiku otsiriza; analonjeza kudzachita zomwezo mwa Yezebeli wauzimu, monga izo zinachitira mwa Yezebeli wachibadwa, mu m'badwo wotsiriza.

382 Ndi chifukwa chake ine—ine ndinapita ku zochuluka chomwecho za Baibulo, kuti ndikatsimikizire izo, kuchitira kuti izo zisasiye funso mmaganizo mwanu. Ngati liripo, inu mundidziwitse ine. Chabwino, mudzandilembere ine kalata kapena kapepala kakang'ono.

383 Ndipo izo zikugwirizana mwangwiro, ngakhale kwa zinyama zikuwononga matupi awo achibadwa mu tsiku lotsiriza, kuwawononga iwo monga zinachitira mu nthawiyo.

384 Mwa kupambana kwa vumbulutso langa, limene linapatsidwa kwa ine ndi Mulungu ndi momwe ananeneratu kuti zikanadzachitidwa, ichi ndi Choonadi cha okwera pa akavalo anayi amenewo, mwa kukhoza kumene ine ndikudziwa.

385 Kodi inu mukuganiza chiyani za Yesu?

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

386 Tsopano kumbukirani, wopanda... (Ndi zimenezo; kazipitirirani; izo ziribwino.) Popanda malingaliro oyipa pa anthu aliwonse a mu bungwe lililonse! Chifukwa, Mulungu ali nawo ana mu kachitidwe ka Chikatolika. Iye ali nawo ana mu kachitidwe ka Chimethodisti. Iye ali nawo ana mu kachitidwe ka Chibaptisti. Ndi angati a iwo, iwo onse machitidwe osiyanasiyana awo, ali kuyimiridwa pano usikuuno, amene anatuluka kuchokera mmenemo pamene inu munawona Kuwala? Tiyeni tiwone manja anu. Tsopano, kumbukirani, kuli anthu kunja uko ndendende ngati inu. Koma ndi kachitidweko kamene kamapha, mwaona. Ndi mzimu wotsutsakhristu umene potsiriza umawatengera iwo ku malo mpaka iwo samamvanso Choonadi.

387 Ndipo mukukumbukira usiku wina, pamene ine ndinkadutsa kupyola mu kusindikiza? Ngati munthu amva kuyitana kwa ufulu, ndipo iye nkukana kupita ali mfulu, iye ankatengedwera ku nsanamira ndipo chisongole chinkabowola khutu lake. Khutu ndiko kumene iwe umamvera. “Ndipo

chikhulupiro chimadza pa kumva.” Ndiye ngati iye awamva Iwo, ndipo nkukana kuvomereza ufulu wake, ndiye iye ali . . . ayenera kumutumikira bwana wake wachipembedzo kwa moyo wake wonse. Amen.

388 Oh! Oh, mai! Kodi Iye siali wodabwitsa?

Ndimkonda Iye, ine . . .

Tiyeni tingokweza manja athu tsopano ndi kumupembedza Iye.

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
(Ulemelero!)

Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

389 Tsopano ingoweramitsani mutu wanu, ndipo tiyeni timupembedze Iye tsopano pamene ife tikuying’ung’uza iyo.

390 Ambuye, tiri othokoza bwanji ife! Ndine wokondwa kwambiri, Ambuye, wokondwa kwambiri chifukwa cha Inu ndi anthu Anu. O Ambuye, Inu munagula chipulumutso chathu pa Kalvare. Ife tikuchilandira icho mokondwera, Ambuye.

391 Tsopano tiyeseni ife, Ambuye, mwa Mzimu Wanu. Ndipo ngati pangakhale choyipa chirichonse pakati pathu, Ambuye, kusakhulupirira kulikonse kwa Mawu, munthu aliyense muno, Atate, amene sangavomereze lonjezo lirilonse la Mulungu ndi “ameni”; mulole kuti Mzimu Woyera utsike pansi tsopano, Wokwera pakavalo woyera, pamene Mzimu Wake, Mzimu wa Khristu, pamaso pa wotsutsakhristu, ndi kudzayitana a Iye Mwini. Ayitanireni iwo atuluke, Ambuye.

392 Mulole tsopano kuti iwo alape, abwere mwamsanga kwa Inu ndi kudzadzazidwa ndi Mafuta ndi vinyo; ndi kusinthidwa kuchokera ku mkanjo wachipembedzo uwo wa imfa ya Kaini, nkupita ku mkanjo woyera ngati chipale wa Moyo Wamuyaya, woperekedwa ndi Mkwati. Ndiyeno iwo adzapita ku Phwando la Chikwati tsiku lina, mu Mawu otsimikiziridwa a chiukitsiro. Perekani izi, Ambuye. Fufuzani mitima, pamene anthu akuyembekezera pa Inu. Kudzera mu Dzina la Yesu!

393 Tsopano, ingofufuzani mtima wanu, m’bale wanga, mlongo wanga, mzanga. Ine ndakhala ndi inu kwa nthawi yayitali. Izi ndi pafupifupi zaka sarte-firii. Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye chimene sichinadzachitike? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Fufuzani Khristu tsopano pamene inu muli nawo mwayi wotero. Izo zikhoza kubwera posachedwa pompa pamene inu simungakhoze kudzachita icho. Mukuona? Iye akhoza kusiya mpando, nthawi iliyonse, wa kupembedzera Kwake; zitatero inu mukhoza kudzalira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kudzapondaponda, inu mukhoza kudzayankhula mmalirime, inu mukhoza kudzathamanga chokwera ndi chotsika pansu,

inu mukhoza kudzachita chirichonse chimene inu mungafune kudzatero, ndi kujowina mpingo uliwonse mdziko, sipadzakhala chirichonse, sipadzakhalanso bulitchi ya lanu—ya tchimo lanu. Ndiye inu mudzachita chiyani, inu mudzakhala pati ndiye?

³⁹⁴ Chabwino, ine ndikukhulupirira, ndi mtima wanga wonse, mpandowo udakali wotsegulabe. Ine ndikukhulupirira Iye akadali pa Mpandowachifumu wa Mulungu. Koma posachedwapa Iye adzukupapo tsopano, ndipo adzatulukira, kudzatenga zomwe Iye waziwombola. Iye akuchita ntchito ya Muwomboli Wachibale, pamene Rute akuyembekezera.

³⁹⁵ Koma posachedwapo, inu mukudziwa, Boazi atatha kuchita ntchito ya wachibale, kenako iye anabwera ndi kudzatenga zomwe zinali zake. Ndipo ndicho ndendende chimene Baibulo linati Iye anachita, “Iye anatulukira ndipo anatenga Bukhulo.” Akatero kupembedzera kwatha; Iye wachokapo pa Mpandowachifumu; palibenso Magazi pa Mpando Wachifundo. Ndiyeno ndi chiyani chimenecho? Mpando Wachiweruzo.

³⁹⁶ Musalole kuti zidzayankhulidwe, ena a masiku awa, “Ine ndimaganza kuti Mkwatulo umayenera kubwera.” Ndi kudzamva Liwu likunena, moyankha, “Zachitika kale.” Mulungu akuthandizeni inu!

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu.

³⁹⁷ M'bale Neville, bwerani, kuti mutibalalitse kapena chirichonse chimene inu muyenera kuchita. Mulungu akudalitsemi inu, mpaka mawa usiku. [M'bale Neville akupemphera—Mkonzi]. 

63-0321 Chisindikizo Chachinayi
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org